# TAONANI Ali Nkudza

## Chodzinenera cha Kabukhu Aka

Pali mipingo yosiyanasiyana yambiri m'dziko lapansi, ndipo mpingo uli wonse pa wokha umakhulupirira kuti ukuphunzitsa choonadi cha m'Bukhu Lopatulika. Koma kuonetsetsa mipingoyi ili ndi ziphunzitso zosiyanasiyana zomwe mkati mwake muli maphunzitso malangizo a anthu.

Kwa zaka zochuruka tsopano bungwe la Mgwirizano wa Mipingo ya Dziko Lapansi (WCC) ndi mabungwe ena akhala akuyesetsa kuyanjanitsa mipingo yonse pogwiritsa ntchito ziphunzitso zomwe ndi zofanana. Koma mpaka lero cholinga chao sichikutheka.

M' kabukhu mukuwerengaka muli mitu ya ziphunzitso yosiyanasina za m'Bukhu Lopatulika zofunikira pa moyo wa chikhristu. Mulinso maulosi a zinthu za mtsogolo. Ulosi wa pa Chibvumbulutso 13:11-18 ukunena za dziko la Amerika kuti lidzakhala mtundu wa ufulu ndi mtendere – mtundu wopangidwa ndi anthu, wa anthu komanso woyendetsedwa ndi anthu – ndiponso kuti lidzakhala ndi mpingo wopanda utsogoleri wa Papa ndi boma lopanda mfumu. Koma chomvetsa chisoni, dziko'lo lidzalankhula ngati chinjoka. Kudzera m'machitidwe a ziwanda ndi ziphunzitso zonama lidzatsogolera anthu kukhulupirira bodza, kuti Mulungu anasintha Sabata kuchokera pa Saturday, tsiku la chisanu ndi chiwiri la pa mulungu, kukhala pa Sunday, tsiku loyamba la pa mulungu. Anthu a ku Amerika adzakakamiza nyumba yao ya Malamulo ya Kongeresi kusintha Malamulo oyendetsera dziko'lo. Pomwepo lamulo la Sunday lidzakhazikitsidwa, ndipo koyambirira chilango chakuswa lamulo'li chidzakhala kungolipira ndalama, kenaka kuikidwa mndende, kenaka kuphedwa kumene. Bukhu Lopatulika likulitcha lamulo la Sunday CHIZINDIKILO CHA CHIROMBO. Maiko onse okhala pa dziko lapansi adzakhazikitsanso lamulo'li potsanzira dziko la Amerika.

Chisautso choopsya chomwe chakhala chikunenedwa chija chikudza mofulumira, ndipo monga imachitira mbala usiku, chikufika pa dziko lapansi modzidzimutsa. Anthu a dziko lapansi adzagawika MMAGULU AWIRI – la iwo akusunga Sabata ndi la iwo akusunga Sunday.

Okondedwa awerengi, kabukhu aka kalembedwa kukuthandizani kupanga chisankho choyenera m'moyo uno, kuti mukhale okonzeka za moyo wosatha umene ulinkudza pakubwera kwa chiwiri kwa posachedwa kwa Ambuye wathu Yesu Khristu.

## Phindu La Kuwerenga Bukhu Lopatulika

Bukhu Lopatulika likudzichitira umboni kuti linachokera kwa Mulungu. Palibenso bukhu lina limayankha mafunso a m'malingaliro, kapena kukwaniritsa zokhumba za mtima monga limachitira Bukhu Lopatulika. Liri Bukhu la anthu a mitundu yonse, lokhala ndi mayankho ku machitidwe osiyanasiyana, ndi lodzala ndi chidziwitso cha kuunika ndi chiyero ku moyo wa munthu.

M'Bukhu Lopatulika timapezamo bvumbulutso la Mulungu wa moyo. Kuliwerenga mwa chikhulupiriro liri ndi mphamvu ya kuusintha moyo. Mu mbiri yake yonse dzanja la Mulungu lakhala liri pa Bukhu'li, kulitchinjiriza kuti liunikire dziko lapansi.

Chinanso dziko lapansi, linapatsidwa Mau a Mulungu'wa, kuti alikonzetsere kulalikira kwa anthu onse uthenga wotsiriza, wa kutha kwa ufumu wa uchimo ndi wa kubwera kwa Ambuye m'ulemelero: "Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu a mitundu yonse; ndipo pomwepo chidzafika chimariziro." Mateyu 24:14.

Monga chotitsogolera, Bukhu Lopatulika liribe lina lopikisana nalo. Limapatsa mtendere wa mumtima m'chikhulupiriro ndi chiyembekezo chozikika za mtsogolo. Limapatsa mayankho ku mabvuto akuru a moyo uno ndi zotsatira zake, ndi kuulimbikitsa kukhala m'chiyero, m'chipiriro, ndi m'ntchito zabwino. Limaudzadza mtima ndi chikondi cha Mulungu komanso chikhumbokhumbo chakuchitira anthu ena zabwino, ndipo limatikonzetsera kukhala a phindu m'moyo uno ndi m'moyo wa kwathu kumwamba. Limatitsimikizira zakufunikira kwa moyo wathu potionetsera za nsembe imene inaperekedwa kutipulumutsa. Limationetsera njira imodzi yokhayo imene tingagonjetsere tchimo, ndikutiphunzitsa za malamulo angwiro anapatsidwawo ku nthawi za nthawi. Limalosera za mtsogolo ndi kutithandiza momwe tingakhalire m'chiyembekezo choyenera. Limaulimbiktsa moyo wathu kuima pa choonadi m'nthawi ya mayesero ndi mazunzo.

Kodi lemba liri lonse lipindulitsa pa chiyani?

"Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitso, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha m'chilungamo." 2 Timoteo 3:16.

Nanga cholinga cha Mulungu potipatsa Mau ake chinali chiyani?

"Kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kuchita ntchito iri yonse yabwino." Ndime 17.

Nanga anthu amene ananenera za Mulungu'wa anatsogozedwa ndi yani?

"Pakuti kale lonse chinenero sichinadza ndi chifuniro cha munthu; koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhula." 2 Petro 1:21.

Nanga chifukwa chinanso ndi chiti chomwe Mau a Mulungu analembedwera?

"Pakuti zonse zinalembedwa kale zinalembedwa kutilangiza, kuti mwa chipiriro ndi chitonthozo cha malembo, tikhale ndi chiyembekezo." Aroma 15:4.

Nanga Khristu anati chiyani zakufunikira kwa kuwerenga Mau a Mulungu?

"Musanthula m'malembo, popeza muyesa kuti momwemo muli nao moyo wosatha; ndipo akundichitira Ine umboni ndi iwo omwewo." Yohane 5:39.

Nanga chikhulupiriro cha Yesaya Mneneri chinazikika bwanji pa umuyaya wa Mau a Mulungu?

"Udzu unyala, duwa lifota, koma Mau a Mulungu wathu adzakhala nthawi zachikhalire." Yesaya 40:8.

Ndi chinthu cha chipambano chiti chimene Khristu anachichita kwa akuphunzira ake watangouka kwa akufa?

"Ndipo anawatsegula mitima yao, kuti adziwitse malembo." Luka 24:45.

## Mphamvu M' Mau a Mulungu

Nanga Khristu anawadzudzula motani anthu amene, ingakhale anawerenga mau a Mulungu, analibe chidwi chofuna kuwamvetsetsa?

"Koma Yesu anayankha, nati kwa iwo, Mungolakwa osadziwa malembo, kapena mphamvu za Mulungu." Mateyu 22:29

Ndi ndani omwe Yesu anati ndi odala?

"Koma Iye anati, Inde, koma odala iwo akumva mau a Mulungu, nawasunga." Luka 11:28.

Kodi chotsatira cha ziphunzitso za bodza chimakhala kupembedza kwa mtundu wanji?

"Koma andilambira Ine kwachabe, ndi kuphunzitsa maphunzitso malangizo a anthu." Mateyu 15:9.

Nanga ndi ziphunzitso za mtundu wanji zomwe zidzasokeretsa anthu ambiri m'masiku otsiriza?

"Koma Mzimu anena monenetsa, kuti m'masiku otsiriza ena adzataya chikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosokeretsa ndi maphunzitso a ziwanda." 1 Timoteo 4:1. werenganinso 2 Petro 2:1.

Ndi kwa ndani komwe anthu adzatembenukira ndi kutchera makutu awo?

"Pakuti idzafika nthawi imene sadzalola chiphunzitso cholamitsa; komatu poyabwa m'khutu adzadziunjikitsa aphunzitsi monga mwa zilakolako za iwo okha: ndipo



**"Taonani, akudza ndi mitambo; ndipo diso iri lonse lidzampenya Iye."** Chibvumbulutso 1:7.

adzalubza dala pachoonadi, nadzapatukira kutsata nthanu zachabe." 2 Timoteo 4:3-4.

Nanga chiphunzitso chingadziwike bwanji kuti ndi choona kapena cha bodza?

"Yesani zonse; sungani chokomacho." 1 Atesalonika 5:21.

Nanga Mau a Mulungu amamchitira chiyani munthu amene akuwakhulupirira?

"Ndi kuti kuyambira ukhanda wako wadziwa malembo opatulika, okhoza kukupatsa nzeru kufikira chipulumutso, mwa chikhulupiriro cha mwa Khristu Yesu." 2 Timoteo 3:15.

Kodi ife timapatulidwa ndi chiyani?

"Patulani iwo m'choonadi; mau anu ndi choonadi." Yohane 17:17.

Kodi ophunzira enieni a Yesu ndi anthu otani ndipo choonadi chimawachitira chiyani ?

"Ngati mukhala inu m'mau anga, muli akuphunzira anga ndithu; ndipo mudzazindikira choonadi, ndipo choonadi chidzakumasulani." Yohane 8:31-32.

Nanga chikhalidwe cha Mau a Mulungu ndi chotani?

"Pakuti mau a Mulungu ali amoyo, ndi ochitachita, ndi akuthwa koposa lupanga lakuthwa konsekonse, napyoza kufikira kugawira moyo ndi mzimu, ndi zimfundo ndi mafuta a m'mafupa, nazindikiritsa zolingirira ndi zitsimikizo za mtima." Ahebri 4:12.

Okhulupirira amakonzedwa ndi chiyani?

"Mwakhala okonzeka tsopano inu chifukwa cha mau amene ndalankhula ndi inu." Yohane 15:3.

Nanga mnyamata angalungamitse bwanji njira yake?

"Mnyamata adzayeretsa mayendedwe ake bwanji? Akawasamalira monga mwa mau anu." Masalmo 119:9.

## Kuposa kwa Pemphero

Kodi wolemba Masalmo akumlankhula Mulungu m'mau otani?

"Wakumva pemphero Inu, Zamoyo zonse zidzadza kwa Inu." Masalmo 65:2.

Ndi pakuchita chiyani pomwe tikulonjezedwa kulandira madalitso?

"Pemphani, ndipo chidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo chidzatsegulidwa kwa inu; pakuti yense wakupempha alandira; ndi wakufunayo apeza; ndi kwa wogogodayo chitsegulidwa." Mateyu 7:7-8.

Dziwani ichi: Pemphero ndiko kuutsegula mtima kwa Mulungu monga timachitira kwa bwenzi. Pemphero silimamsintha Mulungu; koma limatisintha ife kudzanso ubale wathu ndi Mulungu. Limatiika ife m'machitidwe oti tilandire mdalitso, ndiponso m'makhalidwe omwe mosakaika Mulungu amatipatsa zomwe tikupemphazo.

Ndi m'machitidwe osayenera ati omwe wolemba Masalmo akuti Mulungu sangamvere pemphero?

"Ndikadasekera zopanda pake m'mtima mwanga, Ambuye sakadandimvera." Masalmo 66:18. Werenganinso Yesaya 59:1-2; Yakobo 4:3.

Ndi pemphero la munthu wotani lomwe Solomo akuti limamnyansa Mulungu?

"Wopewetsa khutu lake kuti asamve chilamulo, ngakhale pemphero lake linyansa" Miyambo 28:9.

Kodi Khristu anatiphunzitsa kuti tipempherereNso ingakhale ayani?

"Koma Ine ndinena kwa inu, Kondanani nao adani anu, ndi kupempherera iwo akuzunza inu." Mateyu 5:44.

Nanga ife tingawapewe bwanji mayesero?

"Dikirani ndi kupemphera, kuti mungalowe m'kuyesedwa: mzimutu uli wakufuna, koma thupi liri lolefuka." Mateyu 26:41.

Nanga munthu apemphere bwanji kuti alandire?

"Koma apemphe ndi chikhulupiriro, wosakaika konse; pakuti wokaikayo afanana ndi pfunde la nyanja lotengeka ndi mphepo ndi kuwinduka nayo. Pakuti asayese munthu uyu kuti adzalandira kanthu kwa Ambuye." Yakobo 1:6-7. Werenganinso Marko 11:24.

Dziwani ichi: Pemphero ndi pfungulo m'dzanja la munthu wa chikhulupiriro lotsegulira nyumba yosungiramo, momwe mumakhala madalitso osawerengeka a Iye Wam'mwambamwamba.

Kodi tikuuzidwa kuti tidikire tikuchita chiyani?

"Koma chitsiriziro cha zinthu zonse chiri pafupi; chifukwa chake khalani anzeru, ndipo dikirani m'mapemphero." 1 Petro 4:7.

Tipemphere kokwanira kangati?

"Pempherani kosaleka." 1 Atesalonika 5:17; "limbikani chilimbikire m'kupemphera." Aroma 12:12.

## Chilengedwe ndi Mlengi

Ndi ndani analenga kumwamba ndi dziko lapansi?

"Pachiyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi." Genesis 1:1.

Kodi Mulungu anagwiritsa ntchito chiyani polenga kumwamba ndi dziko lapansi?

"Zakumwamba zinalengedwa ndi mau a Yehova; ndipo ndi mpweya wa m'kamwa mwake khamu lao lonse. Amaunjika madzi a m'nyanja monga mulu: Amakundika zakudya mosungiramo. Dziko lonse lapansi liope Yehova: ponse pali anthu achite mantha chifukwa cha Iye. Pakuti ananena, ndipo chinachitidwa; Analamulira, ndipo chinakhazikika." Masalmo 33:6-9.

Kudzera mwa ndani momwe Mulungu analenga zinthu zonse?

"Pakuti mwa Iye (Mwana), zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando ya chifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa Iye ndi kwa Iye." Akolose 1:16. Yohane 1:3. werenganinso Ahebri 1:1-2.

Cholilengera dziko lapansi Mulungu chinali chiyani?

"Pakuti atero Yehova amene analenga kumwamba, Iye ndiye Mulungu amene anaumba dziko lapansi, nalipanga; Iye analikhazikitsa, sanalilenga mwachabe; Iye analiumba akhalemo anthu." Yesaya 45:18.

Kodi Mulungu anawatenga kuti anthu amene anadzadza nalo dziko lapansi limene Iye analilenga?

"Ndipo Yehova Mulungu anaumba munthu ndi dothi lapansi, nauzira mpweya wa moyo m'mphuno mwake; munthuyo nakhala wamoyo." Genesis 2:7.

Nanga munthu analengedwa m'chifanizo cha ndani?

"Mulungu ndipo adalenga munthu m'chifanizo chake, m'chifanizo cha Mulungu adamlenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi." Genesis 1:27.

Zinthu zonse zidalengedwa ndi Khristu.

"Pakuti mwa Iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yachifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa Iye ndi kwa Iye. Ndipo Iye ali woyamba wa zonse, ndipo zonse zigwirizana pamodzi mwa Iye. Ndipo Iye ali mutu wa thupi, Eklesiayo; ndiye chiyambi, wobadwa woyamba woturuka mwa akufa; kuti akakhale Iye mwa zonse woyambayamba." Akolose 1:16-18.

Ndi lemba liti lomwe likutsimikizira momveka bwino kuti ndi mphamvu yakulenga ya Mulungu yomwe imasintha moyo wa wokhulupirira?

"Pakuti ife ndife chipango chake, olengedwa mwa Khristu Yesu, kuchita ntchito zabwino, zimene Mulungu anazipangilatu, kuti tikayende m'menemo." Aefeso 2:10.

## Magwero a Uchimo

Kodi mkangano wapakati pa Khristu ndi Satana ukufotokozedwa bwanji?

"Ndipo munali nkhondo m'mwamba. Mikayeli ndi angelo ake akuchita nkhondo ndi chinjoka; chinjokanso ndi angelo ake chinachita nkhondo; ndipo sichinalakika, ndipo sanapezekanso malo ao m'mwamba. Ndipo chinaponyedwa pansi chinjoka chachikuru, njoka yokalambayo, iye wotchedwa mdierekezi ndi Satana, wonyenga wa dziko lonse; chinaponyedwa pansi kudziko, ndi angelo ake anaponyedwa naye pamodzi." Chibvumbulutso 12:7-9.

Dziwani ichi: Mkangano uwu unayambira kumwamba ndipo ukupirirabe pa dziko lapansi.

Unayambitsidwa ndi ndani?

"Iye wochita tchimo ali wochokera mwa mdierekezi, chifukwa mdierekezi anachimwa kuyambira pachiyambi." 1 Yohane 3:8.

Mdierekezi anakhala wakupha kuyambira liti?

"Inu muli ochokera mwa atate wanu mdierekezi, ndipo zolakalaka zake za atate wanu mufuna kuchita. Iyeyu anali wambanda kuyambira pachiyambi, ndipo sanaima m'choonadi, pakuti mwa iye mulibe choonadi. Pamene alankhula bodza, alankhula za mwini wake; pakuti ali wabodza, ndi atate wake wa bodza." Yohane 8:44.

Kodi Satana anali wochimwa chilengedwe iye?

"Unali wangwiro m'njira zako chilengedwere iwe, mpaka chinapezeka mwa iwe chosalungama." Ezekieli 28:15.

Mau a pa Yohane 8:44 akuti iye "sanaima m'choonadi," akutionetsera kuti nthawi ina Satana anakhalapo wangwiro, ndiponso m'choonadi. Petro akufotokoza za "angelo adachimwawo" (werengani 2 Petro 2:4); ndipo Yuda akunena za "angelonso amene sanasunga chikhalidwe chao choyamba." Yuda 6. Angelo awa akuonetsedwa kuti anakhalapo opanda uchimo nthawi ina yake.

Ndi m'mau atinso momwe Khristu akutitsimikizira kuti Satana ndiye magwero a uchimo?

"Pomwepo Iye adzanena kwa iwo a ku dzanja lamanzere, Chokani kwa Ine otembereredwa inu, ku moto wa nthawi zonse wokolezedwera mdierekezi ndi amithenga ake." Mateyu 25:41.

## Kusiyana kwa Satana ndi Yesu

Ndi chiyani chidampangitsa Satana kuti aukire, achimwe, ndi kugwa?

"Unadzikuza mtima chifukwa cha kukongola kwako, waipsa nzeru zako; chifukwa cha kuwala kwako ndakugwetsa pansi, ndakuika pamaso pa mafumu, kuti akupenye." Ezekieli 28:17. "Ndipo iwe unati mumtima mwako, Ndidzakwera kumwamba, ndidzakweza mpando wanga wachifumu pamwamba pa nyenyezi za Mulungu; ndidzakhala pamwamba pa phiri la khamu, m'malekezero a kumpoto; ndidzakwera pamwamba pa mitambo, ndidzafanana ndi Wam'mwambamwamba." Yesaya 14:13-14.

Nanga ndi chifukwa chiyani atangogwetsedwa Satana nthawi

yomweyo kunalalikidwa za tsoka ku dziko lapansi?

"Tsoka mtunda ndi nyanja, chifukwa mdierekezi watsikira kwa inu, wokhala nao udani waukuru, podziwa kuti kamtsalira kanthawi." Chibvumbulutso 12:12.

"Ndinaona Satana alinkugwa ngati mphenzi wochokera kumwamba." Luka 10:18.

## Kuchimwa kwa Munthu

Kodi uchimo ndi imfa zidalowa liti m'dziko lapansi?

"Chifukwa chake, monga uchimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi [Adamu], ndi imfa mwa uchimo; chotero imfa inafikira anthu onse, chifukwa kuti onse anachimwa." Aroma 5:12.

Kodi Kaini atamupha mphwake Mulungu anamdzudzula ndi mau oti chiyani?

"Ukachita zabwino, sudzalandiridwa kodi? Ukaleka kuchita zabwino, uchimo ubwatama pakhomo…Ndipo Iye (Mulungu) anati, Wachita chiyani? Mau a mwazi wa mphwako andipfuulira Ine ku nthaka. Tsopano ndiwe wotembereredwa kunthaka…" Genesis 4:7-11.

Ndi themberero la mtundu wanji lomwe linaperekedwa monga chotsatira cha kupha koyambako?

"Yehova ndipo anati kwa Kaini… Tsopano ndiwe wotembereredwa kunthaka, imene inatsegula pakamwa pake kulandira pa dzanja lako mwazi wa mphwako; pamene udzalima panthaka siidzaperekanso kwa iwe mphamvu yake." Genesis 4:9,11-12.

Nanga dziko lapansi ndi zomera zake linakhuzidwa bwanji ndi kuchimwa kwa Adamu?

"Nthaka ikhale yotembereredwa chifukwa cha iwe; m'kusauka udzadyako masiku onse a moyo wako: minga ndi mitula idzakubalira iwe.." Genesis 3:17-18.

Nanga mphotho yake ya uchimo ndi chiyani?

"Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi imfa." Aroma 6:23. "Chifukwa pa tsiku lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu." Genesis 2:17. "Moyo wochimwawo ndiwo udzafa." Ezekieli 18:4.

Kodi akuti tchimo ndiko kutani?

"Yense wakuchita tchimo achitanso kusayeruzika; ndipo chimo ndiko kusayeruzika." 1 Yohane 3:4.

Ndi chiyani chomwe chimatsogolera kukuchimwa?

"Pamenepo chilakolako chitaima, chibala uchimo." Yakobo 1:15. "Chinthu chiri chonse chosaturuka m'chikhulupiriro, ndicho uchimo." Aroma 14:23.

Choyenera kudziwa: Timamlakwira kapena kusamvera Mulungu tikamalephera kudalira kapena kukhulupirira pa Iye.

## Mphotho Ya Uchimo

Nanga mapeto ndi mphotho yake ya uchimo ndi chiyani?

"Uchimo utakula msinkhu, ubala imfa." Yakobo 1:15.

Munthu angapewe bwanji chilango cha imfachi?

"Koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha mwa Khristu Yesu Ambuye wathu." Aroma 6:23.

## Mphatso ya Mpulumutsi

Ndi kwa anthu otani komwe mphatsoyi imapatsidwa?

"Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wokhulupirira Iye asataike, koma akhale nao moyo wosatha." Yohane 3:16.

Akuti Mphatso ya Mpulumutsiyi imalandiridwa mu njira yanji?

"Wokhulupirira Iye saweruzidwa; wosakhulupirira waweruzidwa ngakhale tsopano, chifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu." Yohane 3:18.

"Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lake." Yohane 1:12.

## Kodi Uchimo ndi chiyani?

Kodi Bukhu Lopatulika likuufotokoza bwanji uchimo?

"Yense wakuchita uchimo achitanso kusayeruzika; ndipo tchimo ndiko kusayeruzika. Ndipo mudziwa kuti Iyeyu anaonekera kudzachotsa machimo; ndipo mwa Iye mulibe uchimo." I Yohane 3:4-5.

Nanga zotsatira za tchimo lochitidwa mwadala ndi chiyani?

"Pakuti tikachimwa ife eni ake, titatha kulandira chidziwitso cha choonadi, palibenso nsembe ya kwa machimo, koma kulindira kwina koopsya kwa chiweruziro, ndi kutentha kwake kwa moto wakuononga otsutsana nao." Ahebri 10:26-27.

## Malamulo a Mulungu

Kodi Mulungu anazindikiritsa bwanji malamulo ake kwa anthu ake?

"Pamenepo Yehova ananena ndi inu ali pakati pa moto; munamva kunena kwa mau, osaona maonekedwe, koma kunenako. Pamenepo nakufotokozerani chipangano chake, chimene anakulamulirani kuchichita, ndiwo Mau Khumi; nawalemba pa magome awiri amiyala." Deuteronomo 4:12-13. Werenganinso Numeri 9:13-14 Za Malamulo Khumi werengani Eksodo 20:1-17.

Ndi ofunikira chotani kodi malamulo amenewa?

"Opa Mulungu, musunge malamulo ake; pakuti choyenera anthu onse ndi ichi." Mlaliki 12:13.

Nanga chikhalidwe cha malamulo a Mulungu ndi chotani?

"Chotero chilamulo chiri choyera, ndi chilangizo chake nchoyera, ndi cholungama, ndi chabwino…Pakuti tidziwa kuti chilamulo chiri chauzimu; koma ine ndiri wathupi wogulitsidwa kapolo wa uchimo." Aroma 7:12,14.

Kodi ndi chiyani chomwe chikutsimikizira kuti Malamulo Khumi, omwe analankhulidwa ndi kulembedwa pa Phiri la Sinai, ali lamulo la ufulu kwa mkhristu?

"Pakuti amene ali yense angasunge malamulo onse, koma akakhumudwa pa limodzi, iyeyu wachimwira onse. Pakuti iye wakuti, Usachite chigololo, anatinso Usaphe. Ndipo ukapanda kuchita chigololo, koma ukapha, wakhala wolakwira lamulo. Lankhulani motero, ndipo chitani motero, monga anthu amene adzaweruzidwa ndi lamulo la ufulu." Yakobo 2:10-12.

Kodi munthu angathe kumdziwa Mulungu koma osasunga malamulo ake?

"Iye wakunena kuti, Ndimdziwa Iye, koma wosasunga malamulo ake, ali wabodza, ndipo mwa iye mulibe choonadi." 1 Yohane 2:4.

Tingazindikire bwanji kuti tikukonda okhulupirira anzathu?

"Umo tizindikira kuti tikonda ana a Mulungu, pamene tikonda Mulungu, ndi kuchita malamulo ake." 1 Yohane 5:2.

Kodi chikondi cha Mulungu ndi chiyani?

"Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu, kuti tisunge malamulo ake: ndipo malamulo ake sali olemetsa." Ndime 3.

Nanga Khristu anachita nao bwanji malamulo a Atate wake?

"Ine ndasunga malamulo a Atate wanga, ndipo ndikhala m'chikondi chake." Yohane 15:10.

Ngati munthu amene ali mwa Khristu, ayenera woteroyo kuyenda motani?

"Iye wakunena kuti akhala mwa Iye (Khristu), ayeneranso mwini wake kuyenda monga anayendera Iyeyo." 1 Yohane 2:6.

Nanga Yesu anati chiyani za chilamulo ndi kudza kwake pa dziko lapansi?

"Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri: sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa." Mateyu 5:17.

Nanga anaphunzitsa zotani za umuyaya wa chilamulo?

"Pakuti indetu ndinena kwa inu, Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo, kufikira zitachitidwa zonse." Ndime 18.

Nanga Mulungu akuti chiyani kwa anthu za kuswa malamulo ake?

"Pakuti amene ali yense angasunge malamulo onse, koma akakhumudwa pa limodzi, iyeyu wachimwira onse." Yakobo 2:10-12.

## Malamulo ndi Uthenga Wabwino

Kodi ntchito yake ya lamulo ndi chiyani?

"Chifukwa kuti pamaso pake palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo; pakuti uchimo udziwika ndi lamulo." Aroma 3:20.

Paja uthenga wabwino umadziwikanso kuti uli chiyani?

"Pakuti Uthenga Wabwino sundichititsa manyazi; pakuti uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wokhulupirira." Aroma 1:16.

Kodi Khristu akulonjeza chiyani za pangano latsopano?

"Koma tsopano Iye wakulandira chitumikiro chomveka choposa, umonso ali Nkhoswe ya pangano labwino loposa limene likhazikika pa malonjezano oposa…. Pakuti ili ndi pangano ndidzalipangana ndi nyumba ya Israyeli, atapita masiku ajawa, anena Ambuye: Ndidzapatsa malamulo anga kuwalonga m'nzeru zao, ndipo pamtima pao ndidzawalemba iwo." Ahebri 8:6, 10.

Ndi chifukwa ninji chisamaliro cha thupi chiri mdani wa Mulungu?

"Chifukwa chisamaliro cha thupi chidana ndi Mulungu; pakuti sichigonja ku chilamulo cha Mulungu, pakuti sichikhoza kutero." Aroma 8:7.

Kodi munthu mwa iye yekha mosathandizidwa ndi Khristu, angathe kusunga malamulo?

"Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zake; wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala chipatso chambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kanthu." Yohane 15:5. Werenganinso Aroma 7:14-19.

Ndi ndani yekhayo amene Yesu anati angalowe mu ufumu wakumwamba?

"Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakuchitayo chifuniro cha Atate wanga wa Kumwamba." Mateyu 7:21.

Kodi munthu ali yense amaonedwa bwanji ponena za kasungidwe ka malamulo a Mulungu?

"Chifukwa chake yense wakumasula limodzi la malamulo amenewa ang'onong'ono, nadzaphunzitsa anthu chomwecho, adzatchulidwa wamng'onong'ono mu Ufumu wa Kumwamba; koma yense wakuchita ndi kuphunzitsa awa, iyeyu adzatchedwa wamkuru mu Ufumu wa Kumwamba." Mateyu 5:19.

Kodi wokhulupirira ayenera kukhalabe mu uchimo chifukwa cha chisomo?

"Chifukwa chake tidzatani? Tidzakhalabe m'uchimo kodi, kuti chisomo chichuruke? Musatero ai. Ife amene tiri akufa ku uchimo, tikhala bwanji chikhalire m'menemo?" Aroma 6:1-2.

Ndi lemba liti lomwe likukaniratu za kulungamitsidwa mwa ntchito za lamulo?

"Chifukwa kuti pamaso pake palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo; pakuti uchimo udziwika ndi lamulo." Aroma 3:20.

Ndi mu njira iti yomwe okhulupirira mwa Khristu amalungamitsidwa?

"Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemelero wa Mulungu; ndipo ayesedwa olungama kwaulere, ndi chisomo chake mwa chiombolo cha mwa Khristu Yesu." Ndime 23-24.

Ndi munjira ya uzimu iti yomwe Khristu anatanthauzira lamulo la chisanu ndi chimodzi ndiponso lachisanu ndi chiwiri?

"Munamva kuti kunalembedwa kwa iwo akale, Usaphe; koma yense wakupha adzakhala wopalamula mlandu: koma Ine ndinena kwa inu, kuti yense wokwiyira mbale wake wopanda chifukwa adzakhala wopalamula mlandu." Mateyu 5:21-22. "Munamva kuti kunanenedwa, Usachite chigololo; koma Ine ndinena kwa inu, kuti yense wakuyang'ana mkazi kumkhumba, pamenepo watha kuchita naye chigololo mumtima mwake." Ndime 27-28.

## Mazunzo a Khristu

Kodi mneneri anati Khristu anadza kudzamva zowawa zotani?

"Iye anatsenderezedwa koma anadzichepetsa yekha osatsegula pakamwa pake; ngati nkhosa yotsogoleredwa kukaphedwa, ndi ngati mwana wa nkhosa amene ali du pamaso pa omsenga, motero sanatsegula pakamwa pake. Anachotsedwa ku chipsinjo ndi chiweruziro; ndipo ndani adzafotokoza nthawi ya moyo wake? Pakuti walikhidwa kunja kuno; chifukwa cha kulakwa kwa anthu anga Iye anakhomedwa." Yesaya 53:7-8.

Kodi Khristu anadziwiratu nthawi isanakwane za chizunzo chimene adzachilandira?

"Ndipo anadzitengera khumi ndi awiriwo, nati kwa iwo, Taonani tikwera kunka ku Yerusalemu, ndipo zidzakwaniritsidwa kwa Mwana wa munthu zonse zolembedwa ndi aneneri. Pakuti adzampereka kwa amitundu, nadzamseka, nadzamchitira chipongwe, nadzamthira malobvu; ndipo atamkwapula adzamupha Iye; ndipo tsiku lachitatu adzauka." Luka 18:31-33.

Kodi ndi mchitidwe womvetsa chisoni wotani umene asilikari anachitira Khristu?

"Ndipo analuka korona waminga, namveka pamutu pake, namgwiritsa bango mdzanja lamanja lake; ndipo anagwada pansi pamaso pake, namchitira chipongwe, nati, Tikuoneni, Mfumu ya Ayuda! Namthira malobvu, natenga bango, nampanda Iye pamutu." Mateyu 27:29-30.

Atafika naye ku malo anampachikawo, ndi chakumwa cha mtundu wanji chomwe anampatsa Khristu?

"Anammwetsa Iye vinyo wosanganiza ndi ndulu; ndipo Iye m'mene analawa, sanafuna kumwa." Ndime 34.

Ndi pemphero lotani lopempherera iwo anampachikawo lomwe Khristu anaonetsa moyo wachoonadi monga mwa uthenga wabwino – wa chikondi cha pa ochimwa?

"Ndipo Yesu ananena, Atate, muwakhululukire iwo, pakuti sadziwa chimene achita." Luka 23:34.

M'mau otani omwe akuru ansembe ndiponso gulu lonse anamchitira nao chipongwe Yesu ali pa mtanda paja?

"Chomwechonso ansembe akuru, pamodzi ndi alembi ndi akuru anamchitira chipongwe, nati, Anapulumutsa ena, sangathe kudzipulumutsa yekha. Ndiye Mfumu ya Ayuda; atsike tsopano pamtandapo, ndipo tidzamkhulupirira Iye." Mateyu 27:41-42.

Nanga nthawi yowawitsayi inatha bwanji?

"Pamene Yesu tsono analandira vinyo wosasayo anati, Kwatha; ndipo anawerama mutu, napereka mzimu." Yohane 19:30.

## Kuuka m'manda kwa Khristu

"Ndinali wakufa, ndipo taona, ndiri wamoyo kufikira nthawi za nthawi, ndipo ndiri nazo zofungulira za imfa ndi Hade." Chibvumbulutso 1:18.

Atauka kwa akufa, ulauli uwu unadzetsa zotsatira zanji mwa ophunzira?

"Chifukwa chake atauka kwa akufa, akuphunzira ake anakumbukira kuti ananena ichi; ndipo anakhulupirira cholemba, ndi mau amene Yesu ananena." Yohane 2:22.

"Pakuti ndipereka kwa inu poyamba, chimenenso ndinalandira, kuti Khristu anafera zoipa zathu, monga mwa malembo; ndi kuti anaikidwa; ndi kuti anaukitsidwa tsiku lachitatu; monga mwa malembo." 1 Akorinto 15:3-4.

"Ndi kuti anaonekera kwa Kefa; pamenepo kwa khumi ndi awiriwo; pomwepo anaoneka pa nthawi imodzi kwa abale oposa mazana asanu, amene ochuruka a iwo akhala kufikira tsopano, koma ena anagona; pomwepo anaonekera kwa Yakobo; pamenepo kwa atumwi onse." Ndime 5-7.

## Kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro

Kodi Mulungu amamulungamitsa bwanji munthu?

"Kuti poyesedwa olungama ndi chisomo cha Iyeyu, tikayesedwe olowa nyumba monga mwa chiyembekezo cha moyo wosatha." Tito 3:7.

Kodi ndi kudzera mu njira yanji yomwe chisomo ichi chakulungamitsa chimamfikira munthu wochimwa?

"Ndipo tsono popeza tinayesedwa olungama ndi mwazi wake, makamaka ndithu tidzapulumutsidwa mkwiyo wa Mulungu mwa Iyeyu." Aroma 5:9.

Nanga munthu amakulandira bwanji kulungamaku?

"Pakuti timuyesa munthu wolungama chifukwa cha chikhulupiriro, wopanda ntchito za lamulo." Aroma 3:28.

Ndi njira iti yokhayo imene ochimwa angathe kulungamitsidwa kapena kupangidwa oyera?

"Koma podziwa kuti munthu sayesedwa wolungama pa ntchito ya lamulo, koma mwa chikhulupiriro cha Yesu Khristu, ifedi tinakhulupirira kwa Yesu Khristu, kuti tikayesedwe olungama ndi chikhulupiriro cha Khristu, ndipo si ndi ntchito za lamulo; pakuti palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo." Agalatiya 2:16.

Ndi njira iti yomwe zibvute zitani munthu wochimwa sangathe kulungamitsidwa nayo?

"Chifukwa kuti pamaso pake palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo; pakuti uchimo udziwika ndi lamulo." Aroma 3:20.

Nanga imfa ya Khristu ikuchitira motani umboni za ichi?

"Sindichiyesa chopanda pake chisomo cha Mulungu; pakuti ngati chilungamo chiri mwa lamulo Khristu anafa chabe." Agalatiya 2:21.

Nanga anthu omwe akudzilungamitsa ndi ntchito za lamulo akulangizidwa chiyani?

"Mulibe kanthu ndi Khristu, inu amene muyesedwa olungama ndi lamulo; mudagwa posiyana nacho chisomo." Agalatiya 5:4.

Chifukwa chiyani kuti ingakhale anachita ntchito za lamulo, a Israyeli sanapezedwa olungama?

"Koma Israyeli potsata lamulo la chilungamo, sanafikira lamulolo. Chifukwa chanji? Chifukwa kuti sanachitsata ndi chikhulupiriro, koma monga ngati ndi ntchito. Anakhumudwa pa mwala wokhumudwitsa." Aroma 9:31-32.

Ndi chiyani chimadziwika ndi lamulo?

"Pakuti uchimo udziwika ndi lamulo." Aroma 3:20.

Ndi chiyaninso china chomwe chikuchitira umboni za kulungamitsidwa kochitika mwa chikhulupiriro, opanda ntchito za lamulo?

"Koma tsopano chilungamo cha Mulungu chaoneka chopanda lamulo, chilamulo ndi aneneri achitira ichi umboni." Ndime 21.

Kodi chikhulupiriro ndi chofunika bwanji?

"Koma wopanda chikhulupiriro sikutheka kumkondweretsa (Mulungu)." Ahebri 11:6.

Nanga ndi lemba liti lomwe likutionetsera kuti chilungamo cholandiridwa mwa chisomo kudzera m'chikhulupiriro chisatengedwe kukhala tchinga loti tidzichimwira chimwira?

"Chifukwa chake tidzatani? Tidzakhalabe m'uchimo kodi, kuti chisomo chichuruke? Musatero ai. Ife amene tiri akufa ku uchimo, tidzakhala bwanji chikhalire m'menemo?" Aroma 6:1-2.

Kodi chifukwa cha chikhulupiriro tiliyese lamulo la Mulungu lopanda ntchito?

"Potero kodi lamulo tiyesa chabe mwa chikhulupiriro? Msatero ai; koma tikhazikitsa lamulo." Aroma 3:31.

## Kulapa

Kodi ndi ndani akuitanidwa kukulapa?

"Sindinadza Ine kuitana olungama, koma ochimwa kuti atembenuke mtima." Luka 5:32.

Ndi anthu angati omwe ndi ochimwa?

Pakuti tidawaneneza kale Ayuda ndi Ahelene omwe, kuti onsewa agwidwa ndi uchimo." Aroma 3:9.

Ndi mafunso oti chiyani omwe ochimwa amafunsa za chipulumutso chao?

"Tidzachita chiyani amuna inu, abale?" "Ambuye ndichitenji kuti ndipulumuke?" Machitidwe 2:37; 16:30.

Nanga Mau a Mulungu amapereka mayankho otani ku mafunsowo?

"Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu." "Ukhulupirire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka." Machitidwe 2:38; 16:31.

Nanga zotsatira za chisoni cha Mulungu ndi chiyani?

"Pakuti chisoni cha kwa Mulungu chitembenuzira mtima ku chipulumutso." 2 Akorinto 7:10.

Kodi Yohane Mbatizi anati chiyani kwa Afarisi ndi Asaduki pomwe anadza kuti abatizidwe ndi iye?

"Obadwa a njoka inu, ndani anakulangizani kuthawa mkwiyo ulinkudza?" Mateyu 3:7.

Anawauza kuti achite chiyani?

"Onetsani inu zipatso zakuyenera kutembenuka mtima." Ndime 8.

## Kubvomereza ndi Kukhululukidwa

Ndi lonjezano lanji lomwe linaperekedwa kwa obvomereza machimo ao?

"Ngati tibvomereza machimo athu,

ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chiri chonse.” 1 Yohane 1:9.

Nanga ndi zotsatira zosiyana ziti pa iwo akubisa ndi iwo obvomereza machimo ao?

“Wobisa machimo ake sadzaona mwai; koma wakuwabvomereza, nawasiya adzachitidwa chifundo.” Miyambo 28:13.

Mulungu ndi wokonzeka kuchita chiyani kwa onse ofuna chikhululukiro cha machimo ao?

“Pakuti Inu, Ambuye, ndinu wabwino, ndi wokhululukira, ndi wa chifundo chochurukira onse akuitana Inu.” Masalmo 86:5.

Ndi pa ndani pomwe Davide anazika chikhululupiro za chikhululukiro chake?

“Mundichitire ine chifundo, Mulungu, monga mwa kukoma mtima kwanu; monga mwa unyinji wa nsoni zokoma zanu. Mufafanize machimo anga.” Masalmo 51:1.

Atabvomereza tchimo lake, Davide akuti Mulungu anachita chiyani?

“Ndinabvomereza choipa changa kwa Inu; ndipo mphulupulu yanga sindinaibisa. Ndinati, Ndidzaululira Yehova machimo anga; ndipo munandikhululukira choipa cha kulakwa kwanga.” Masalmo 32:5.

Nanga ife tichionetsere bwanji chikhululukiro cha machimo athu cha Mulungu?

“Koma mukhalirane okoma wina ndi mnzake, a mtima wachifundo, akukhululukirana nokha, monganso Mulungu mwa Khristu anakhululukira inu.” Aefeso 4:32.

Ndi kudzera mwa ndani momwe kulapa ndi chikhululukiro cha machimo zimaperekedwa?

“Mulungu wa makolo athu anaukitsa Yesu, amene munamupha inu, ndi kumpachika pa mtengo. Ameneyo Mulungu anamkweza ndi dzanja lake lamanja, akhale Mtsogoleri ndi Mpulumutsi, kuti apatse kwa Israyeli kulapa, ndi chikhululukiro cha machimo.” Machitidwe 5:30-31.

## Mzimu Woyera ndi Ntchito yake

Ndi lonjezano la mtengo wapatali liti lomwe Yesu analipereka kwa ophunzira ake patangotsala nthawi yochepa kuti apachikidwe?

“Ndipo Ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe yina, kuti akhale ndi inu ku nthawi yonse.” Yohane 14:16.

Chifukwa ninji kudali kofunika kuti Khristu achoke? Koma ndinena Ine choonadi ndi inu; kuyenera kwa inu kuti ndichoke Ine; pakuti ngati sindichoka, Nkhoswe sadzadza kwa inu; koma ngati ndipita ndidzamtuma Iye kwa inu.” Yohane 16:7.

Kodi Nkhoswe ameneyu ndi ndani, ndipo anati adzachita chiyani?

“Koma Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m’dzina langa, Iyeyo adzaphunzitsa inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu.” Yohane 14:26.

Chinanso ndi chiyani chimene anati Nkhosweyo adzachichita?

“Ndipo atadza Iyeyo, adzatsutsa dziko lapansi za machimo, ndi za chilungamo, ndi za chiweruziro.” Yohane 16:8.

Kodi ndi dzina linanso liti lomwe Nkhosweyo amadziwika nalo?

“Koma pamene wafika Nkhosweyo, amene Ine ndidzamtuma kwa inu kuchokera kwa Atate, ndiye Mzimu wa choonadi, amene aturuka kwa Atate, Iyeyu adzandichitira Ine umboni.” Yohane 15:26.

Chinanso ndi chiyani chimene Yesu ananena kuti Mzimu wa choonadiyo akadza adzachichita?

“Koma atadza Iyeyo, Mzimu wa choonadi, adzatsogolera inu m’choonadi chonse; pakuti sadzalankhula za Iye mwini; koma zinthu zonse adzazimva, adzazilankhula; ndipo zinthu zirinkudza adzakulalikirani.” Yohane 16:13.

Chifukwa chake ndi chenjezo lanji lomwe likuperekedwa za Mzimu wa choonadiyo?

“Ndipo musamvetse chisoni Mzimu Woyera wa Mulungu, amene munasindikizidwa chizindikilo mwa Iye, kufikira tsiku la maomboledwe.” Aefeso 4:30.

Kodi pamafika pakuti Mzimu wa Mulungu sangathe kupitiriza kulimbana ndi munthu?

“Ndipo anati Yehova, Mzimu wanga sudzakangana ndi anthu nthawi zonse.” Genesis 6:3.

Kodi Davide anapemphera kuti Mulungu asamchitire chiyani?

“Musanditaye kundichotsa pamaso panu; musandichotsere Mzimu wanu Woyera.” Masalmo 51:11.

Ndi ndani anatsogolera aneneri powapatsa iwo mau achinenero?

“Pakuti kale lonse chinenero sichinadza ndi chifuniro cha munthu; koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhula.” 2 Petro 1:21.

Kodi chipatso cha Mzimu ndi chiyani?

“Koma chipatso cha Mzimu ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiriro, chifatso, chiletso.” Agalatiya 5:22-23.

Ndi phunzironso liti lomwe ife tiyenera kukhala ndi chidziwitso chokwanira za ilo?

“Koma za mphatso zauzimu, abale, sindifuna kuti mukhale osadziwa.” 1 Akorinto 12:1.

Ndi mphatso ziti zomwe zikupatsidwa ku mpingo mpaka pano?

“Ndipotu Mulungu anaika ena m’Eklesia, poyamba atumwi, achiwiri aneneri, achitatu aphunzitsi, pomwepo mphatso za machiritso, mathandizo, maweruziro, malilime a mitundu mitundu.” 1 Akorinto 12:28.

## Ubatizo wa Chikhristu

Ndi utumiki uti womwe ukukhuzana kwenikweni ndi chikhulupiriro cha Uthenga Wabwino?

“Ndipo ananena nao, Mukani ku dzko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupirira adzalangidwa.” Marko 16:15-16.

Kodi anthu anaulandira bwanji ulaliki wa Yohane?

“Pamenepo panamturukira iye a ku Yerusalemu, ndi Yudeya lonse, ndi dziko lonse loyandikira ndi Yordano; nabatizidwa ndi iye mu mtsinjewo wa Yordano, alikuulula machimo ao.” Mateyu 3:5-6.

Nanga mu ulaliki wake wa pa Pentekoste mtumwi Petro anauonetsera ubatizo kuti uli njira yolandirira mphatso yanji?

“Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m’dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.” Machitidwe 2:38.

Kudzera mu machitidwe a ubatizo wa chikhristu ndi chiyani chimatsukidwa?

“Ndipo tsopano uchedweranji? Tauka, nubatizidwe ndi kusamba kuchotsa machimo ako, nuitane pa dzina lake.” Machitidwe 22:16. Werenganinso Tito 3:5; 1 Petro 3:21.

Ndi chiyani chenicheni chomwe chimatsuka ndi kuchotsa machimo?

“Kwa Iye amene atikonda ife, natimasula ku machimo athu ndi mwazi wake.” Chibvumbulutso 1:5.

Kodi okhulupirira akabatizidwa m’dzina la Khristu, amambvala ndani?

“Pakuti nonse amene munabatizidwa kwa Khristu mudabvala Khristu.” Agalatiya 3:27.

Kodi anthu amene tikubatizidwa akuti tikubatizidwa mu chiyani cha Khristu?

“Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Khristu Yesu; tinabatizidwa mu imfa yake?” Aroma 6:3.

Nanga ubatizo ukufotokozedwa momveka bwanji?

“Chifukwa chake tinaikidwa m’manda pamodzi ndi Iye mwa ubatizo kulowa muimfa; kuti monga Khristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemelero wa Atate, chotero ifenso tikayende m’moyo watsopano.” Ndime 4.

Mu ubatizo, ife timayanjana bwanji kotheratu ndi Khristu ponena za imfa ndi kuuka kwake kwa akufa?

“Pakuti ngati ife tikhala olumikizidwa ndi Iye m’chifanizo cha imfa yake, koteronso tidzakhala m’chifanizidwe cha kuuka kwake.” Ndime 5.

Ndi funso lanji lomwe mdindo anamfunsa Filipo atangotha kulalikira Khristu kwa mdindoyo?

“Ndipo monga anapita panjira pao, anadza ku madzi; ndipo mdindoyo anati, Taonapo madzi; chindiletsa ine chiyani ndisabatizidwe?” Machitidwe 8:36.

Kuti Filipo am’batize mdindoyo, awiriwo analowa m’chiyani?

“Ndipo anamuuza kuti aimitse gareta; ndi anatsikira onse awiri kumadzi, Filipo ndi mdindoyo; ndipo anambatiza iye.” Ndime 38.

Kumayambiriro kwa Utumiki wake, ndi chitsanzo chanji chomwe Yesu anachipereka kuti chipindulire omtsatira ake?

“Pamenepo Yesu anachokera ku Galileya nadza ku Yordano kwa Yohane, kudzabatizidwa ndi iye.” Mateyu 3:13.

## Mphatso ya Kupatsa

Kodi Khristu anati chiyani za mdalitso wakupatsa?

“M’zinthu zonse ndinakupatsani chitsanzo chakuti pogwiritsa ntchito, kotero muyenera kuthandiza ofoka ndi kukumbuka mau a Ambuye Yesu, kuti anati yekha, Kupatsa kutidalitsa koposa kulandira.” Machitidwe 20:35.

Ndi kusala kwa mtundu wanji komwe ndi kobvomerezeka ndi Mulungu?

“Kodi kumeneko si kusala kudya kumene ndinakusankha…Kodi si ndiko kupatsa chakudya chako kwa anjala, ndi kuti ubwere nao kunyumba kwako aumphawi otayika? Pakuona wamaliseche kuti umbveke, ndi kuti usadzibisire wekha a chibale chako?” Yesaya 58:6-7.

Ndi mu njira inanso iti yomwe ife tikuuzidwa kulemekeza nayo Mulungu?

“Lemekeza Yehova ndi chuma chako, ndi zinthu zako zonsae zoyambirira kucha.” Miyambo 3:9.

Ndi gawo liti la chuma cha munthu lomwe Ambuye akuti ndi lake?

“Limodzi mwa magawo khumi la zonse m’dziko, la mbeu zake za dziko, la zipatso za mtengo, ndilo la Yehova; likhale lopatulikira Yehova.” Levitiko 27:30.

Cholinga cha chachikhumi chinali choti chithandizire ndi kugwira ntchito yanji m’Israyeli?

“Ndipo taonani, ndawaninkha ana a Levi limodzi la magawo khumi mwa zonse m’Israyeli, likhale cholowa chao, mphotho ya pa ntchito yao alikuichita, ntchito ya chihema chokomanako.” Numeri 18:21.

Nanga iwo amene samabwezera

chachikhumi ndi zopereka amapalamula tchimo lanji?

"Kodi munthu adzalanda za Mulungu? Ndipo inu mumandilanda Ine. Koma mumati, Tikulandani zotani? Limodzi limodzi la magawo khumi ndi zopereka." Malaki 3:8.

Ndi pakuchita chiyani pomwe Ambuye akutifunsa kumuyesa Iye, ndipo Iye akutilonjeza mdalitso wochuruka bwanji?

"Mubwere nalo limodzilimodzi lonse la khumi, ku nyumba yosungiramo, kuti m'nyumba mwanga mukhale chakudya; ndipo mundiyese nako tsono, ati Yehova wa makamu, ngati sindikutsegulirani mazenera a kumwamba, ndi kukutsanulirani mdalitso wakuti adzasoweka malo akuulandira. Ndipo ndidzadzudzula zolusa chifukwa cha inu, kuti zisakuonongereni zipatso za nthaka yanu; ngakhale mpesa wanu sudzayoyoka zipatso zake zosacha m'munda, ati Yehova wa makamu." Ndime 10-11.

Ife tipereke ndi mtima wotani?

"Yense achite monga anatsimikiza mtima, si mwa chisoni kapena mokakamiza, pakuti Mulungu akonda wopereka mokondwerera." 2 Akorinto 9:7.

Nanga Khristu akuti chiyani za kupatsa?

"Kupatsa kutidalitsa koposa kulandira." Machitidwe 20:35.

Kodi mphatso ziperekedwe motani kuti zikhale zobvomerezeka?

"Pakuti ngati chibvomerezo chiri pomwepo, munthu alandiridwa monga momwe ali nacho, si monga chimsowa." 2 Akorinto 8:12.

Pamene Khristu anatuma akuphunzira ake kunka akulalikira, kuchiritsa odwala ndi kuukitsa akufa, anawalangiza chiyani?

"Chiritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwa ulere." Mateyu 10:8.

## Thanzi Labwino

Kodi mtumwi Yohane anamfunira Gayo thanzi lotani?

"Wokondedwa, ndipemphera kuti pa zonse ulemere, nukhale bwino, monga mzimu wako ulemera." 3 Yohane 2.

Chifukwa chiyani kuli kofunikira kwambiri kusamalira thanzi la thupi lathu?

"Pakuti munagulidwa ndi mtengo wake wapatali; chifukwa chake lemekezani Mulungu m'thupi lanu." 1 Akorinto 6:20.

Kodi thupi lathu likunenedwa kuti liri chiyani?

" Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri kachisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu? Ndipo simukhala a inu nokha." Ndime 19.

Kodi mtima wa chimwemwe ndi wofunika bwanji za thanzi labwino?

"Mtima wosekera uchiritsa bwino." Miyambo 17:22.

Kodi Mpulumutsi anapatsa bwanji mpumulo kwa ophunzira ake?

"Ndipo Iye ananena nao, Idzani inu nokha padera ku malo achipululu, mupumule kamphindi." Marko 6:31.

Nanga tikulangizidwa kupereka matupi athu motani kwa Mulungu?

"Chifukwa chake ndikupemphani inu, abale, mwa zifundo za Mulungu, kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu." Aroma 12:1.

Ndi chiyani chomwe chidzikhala choyambirira pakunena za kudziletsa?

"Chifukwa chake mungakhale mudya, mungakhale mumwa, mungakhale muchita kanthu kena, chitani zonse ku ulemelero wa Mulungu." 1 Akorinto 10:31.

Ndi chenjezo lanji lomwe likuperekedwa kwa iwo otsogolera anzao kukusadziletsa?

"Tsoka wakuninkha mnzake chakumwa, ndi kuonjezako mankhwala ako, ndi kumledzeretsa." Habakuku 2:15.

Kodi oledzera angalowe mu ufumu wa kumwamba?

"Adama, kapena opembedza mafano....kapena ambala, kapena osirira, kapena oledzera, kapena olalatira, kapena olanda, sadzalowa ufumu wa Mulungu." 1 Akorinto 6:9-10. Werenganinso Chibvumbulutso 21:27.

Kodi chotsatira chimodzi choipitsitsa chakusadziletsa ndi chiyani?

"Usakhale mwa akumwaimwa vinyo, ndi ankhuli osusuka. Pakuti wakumwaimwa ndi wosusukayo adzasauka." Miyambo 23:20-21.

Nanga ndi chenjezo lanji lingaperekedwe za kusuta fodya?

Fodya ali ndi ululu waukuru, choncho ndi woopsa kwambiri.

Choyenera Kudziwa: "Fodya ali ndi ululu wakupha, ndipo kuipitsitsa kwake kumadziwidwa bwino kwambiri ndi onse amene amadziwa bwino za mankhwala, kuti wali mankhwala a ululu wakupha mosanyengerera." M. Orfila, yemwe anakhalapo mkuru wa sukulu ya maphunziro a pa mwamba ya za mankhwala ku Paris.

Chakudya cha poyamba pa chilengedwe, kodi chinali chiyani?

"Ndipo anati Mulungu, Taonani, ndakupatsani inu therere lonse lakubala mbeu liri pa dziko lapansi, ndi mitengo yonse m'mene muli chipatso cha mtengo wakubala mbeu; chidzakhala chakudya cha inu." Genesis 1:29.

Dziwani ichi – Tinapatsidwa, za masamba, njere, zipatso ndi mtedza kukhala chakudya chathu.

Pamene Mulungu anasankha a Israyeli kukhala anthu ake, ndi nyama za mtundu wanji zomwe iwo analetsedwa kuzidya?

Zonse zotchedwazo zodetsedwa. Werengani Levitiko 11 ndi Deuteronomo 14.

## Akufa ali kuti?

Kodi Bukhu Lopatulika limaifotokoza bwanji imfa?

"Koma sitifuna, abale kuti mukhale osadziwa za iwo akugona, kuti mungalire monganso otsalawo, amene alibe chiyembekezo." 1 Atesalonika 4:13. Werenganinso 1 Akorinto 15:18, 20; Yohane 11:11-14.

"Ndipo ambiri a iwo ogona m'pfumbi lapansi adzauka." Danieli 12:2. Werenganinso Mlaliki 3:20; 9:10.

Nanga olungama akufa ali kumwamba komwe akulemekeza Mulungu?

"Pakuti Davide sanakwera Kumwamba ai." Machitidwe 2:34. "Akufa salemekeza Yehova, kapena ali yense wakutsikira kuli chete." Masalmo 115:17.

Kodi munthu akafa amaganizira za Mulungu?

"Pakuti muimfa m'mosakumbukira Inu." Masalmo 6:5.

Nanga munthu wakufa amazindikila zomwe zikuchitika m'banja lake?

"Ana ake aona ulemu osadziwa iye; napeputsidwa, koma osazindikira za iwo." Yobu 14:21.

Munthu akafa amapitiriza kuchita zomwe amalingirira ali ndi moyo?

"Mpweya wake uchoka, abwerera kunka ku nthaka yake; Tsiku lomwelo zotsimikiza mtima zake zitayika." Masalmo 146:4.

Kodi akufa amazindikira za chinthu china chiri chonse?

"Pakuti amoyo adziwa kuti tidzafa; koma akufa sadziwa kanthu bi." Mlaliki 9:5.

Monga iwo amatengako mbali pazochitika ziri zonse za pa dziko?

"Chikondi chao ndi mdano wao ndi dumbo lao lomwe zatha tsopano; ndipo nthawi yamuyaya sagawa konse kanthu kali konse kachitidwa pansi pano." Ndime 6.

Kodi kuuka kwa akufa kudzachitika liti?

"Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka." 1 Atesalonika 4:16.

Uchimo unadzetsa chiyani kwa anthu onse?

"Mwa Adamu onse amwalira." 1 Akorinto 15:22. Werenganinso Aroma 5:12.

Timachita ntchito zochuruka bwanji tikafa?

"Chiri chonse dzanja lako lichipeza kuchichita, uchichite ndi mphamvu yako; pakuti mulibe ntchito ngakhale kulingirira ngakhale kudziwa, ngakhale nzeru, kumanda ulikupitako." Mlaliki 9:10.

Ndi mau a ndani omwe adzadzutsa akufa?

"Musazizwe ndi ichi, kuti ikudza nthawi, imene onse ali m'manda adzamva mau ake, (Yesu) nadzaturukira, amene adachita zabwino, kukuuka kwa moyo; koma amene adachita zoipa kukuuka kwa kuweruza." Yohane 5:28-29.

Imfa itagonjetsedwa idzabetcheredwa ndi mau otani pa nthawi ya mdzukiro?

"Imfawe, chigonjetso chako chiri kuti? Imfawe, mbola yako iri kuti?" 1 Akorinto 15:55.

Nanga olungama oukitsidwa adzakhala ndi matupi angati thupi la ndani?

"Pakuti ufulu wathu uli kumwamba; kuchokera komwenso tilindira Mpulumutsi, Ambuye Yesu Khristu; amene adzasanduliza thupi lathu lopepulidwa, lifanane nalo thupi lake la ulemelero." Afilipi 3:20-21.

## Kukhazikitsidwa kwa Sabata

Kodi Sabata linakhazikitsidwa liti ndiponso ndi ndani?

"Ndipo zinatha kupangidwa za kumwamba ndi dziko lapansi, ndi khamu lao lonse. Tsiku lachisanu ndi chiwiri Mulungu anamariza ntchito yonse anaipanga; ndipo anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri ku ntchito yake yonse." Genesis 2:1-2.

"Mulungu ndipo anadalitsa tsiku lachisanu ndi chiwiri, naliyeretsa limenelo: chifukwa limenelo adapuma ku ntchito yake yonse imene Mulungu anailenga ndi kupanga." Ndime 3.

Chifukwa chiyani kuli kofunikira kulisunga tsiku la Sabata kukhala lopatulika?

"Chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopautlika." Eksodo 20:11.

Dziwani ichi - Sabata ndi chikumbutso cha Chilengedwe. Mulungu anakonza kuti kudzera m'kulisunga ilo munthu adzikumbukira za Iye nthawi zonse kuti ali Mulungu wamoyo, Mlengi wa zinthu zonse Ndi tsiku liti lomwe ndi la Sabata?.

"Tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo la Sabata." Eksodo 20:10.

Kodi Sabata linaikidwanso kukhala lakupembedza?

"Masiku asanu ndi limodzi azigwira ntchito; koma lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata lakupumula, msonkhano wopatulika." Levitiko 23:3.

Dziwani ichi – Msonkhano wopatulika ndiko kusonkhana ndi kupemphera pamodzi anthu onse.

Mulungu akuti anaika Sabata kukhalanso chikumbutso kapena chizindikilo cha chiyani?

"Ndipo ndinawapatsanso masabata

anga akhale chizindikilo pakati pa Ine ndi iwo, kuti adziwe kuti Ine ndine Yehova wakuwapatula." Ezekieli 20:12.

Kodi opulumutsidwa adzasonkhana kangati kupembedza Mulungu?

"Pakuti monga m'mwamba mwatsopano ndi dziko lapansi latsopano limene ndidzalenga, lidzakhalabe pamaso pa Ine, ati Yehova, momwemo adzakhalabe ana anu ndi dzina lanu. Ndipo kudzakhala kuti kuyambira pa mwezi wokhala kufikira ku unzake, ndi kuyambira pa Sabata lina kufikira ku linzake, anthu onse adzafika kudzapembedzera pamaso pa Ine ati Yehova." Yesaya 66:22-23.

Malinga ndi Bukhu Lopatulika, Sabata limayamba nthawi yanji?

"Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku loyamba...Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa tsiku lachiwiri." Etc. Werengani Genesis 1:5, 8,13,19,23,31. "Kuyambira madzulo kufikira madzulo musunge Sabata lanu." Levitiko 23:32. Werenganinso Marko 1:32.

Ali pa dziko lapansi pano Yesu anasunga Sabata?

"Ndipo anadza ku Nazarete, kumene analeredwa; ndipo tsiku la Sabata analowa m'sunagoge, monga anazolowera, naimiriramo kuwerenga m'kalata." Luka 4:16.

Ingakhale Ambuye anali Mlengi, ndiponso Msungi wa Sabata, anazondedwa bwanji za tsiku'li?

"Ndipo alembi ndi afarisi analikumzonda Iye, ngati adzachiritsa tsiku la Sabata; kuti akapeze chomneneza Iye." Luka 6:7.

Nanga Khristu anatsutsana nao bwanji zakasungidwe kao konama ka Sabata?

"Ndipo Yesu anati kwa iwo...kodi nkuloleka tsiku la Sabata, kuchita zabwino, kapena kuchita zoipa? Kupulumutsa moyo, kapena kuuononga?" Ndime 9.

## Tsiku la Ambuye

Kodi ndi pa tsiku lanji lomwe Yohane akuti anagwidwa ndi Mzimu?

"Ndinagwidwa ndi Mzimu tsiku la Ambuye." Chibvumbulutso 1:10.

Nanga malamulo akuti tsiku la Ambuye ndi liti?

"Koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako." Eksodo 20:10.

Polankhula kudzera mwa mneneri Yesaya za Sabata lake la tsiku chisanu ndi chiwiri Mulungu akulitcha chiyani?

"Tsiku langa lopatulika." Yesaya 58:13.

Ndi tsiku liti lomwe Yohane akuoneka kuti anagwidwa ndi Mzimu?

La chisanu ndi chiwiri, ngati amatanthauza za mulungu monga timaudziwira.

Dziwani ichi – Malingana ndi Bukhu Lopatulika palibe tsiku lina liri lonse lomwe Mulungu analinenapo kuti ndi lake kupatula tsiku lachisanu ndi chiwiri.

Paja Yesu analisunganso?

"Ndipo tsiku la Sabata analowa m'sunagoge, monga anazolowera, naimiriramo kuwerenga m'kalata." Luka 4:16. "Ine ndasunga malamulo a Atate wanga." Yohane 15:10.

Kodi pambuyo pa imfa yake ophunzira a Khristu anasungabe Sabata?

"Ndipo anapita kwao, nakonza zonunkhira ndi mafuta abwino. Ndipo pa Sabata anapumula monga mwa lamulo." Luka 23:56.

"Kuti onse alemekeze Mwana, monga alemekeza Atate." Yohane 5:23. "Ine ndi Atate ndife amodzi." Yohane 10:30.

Dziwani ichi – Liu "onse" liimira mtundu wonse wa anthu.

Kodi Yesu anati Mwana wa munthu ndi Mbuye wa chiyaninso?

"Pakuti Mwana wa munthu ali mwini tsiku la Sabata." Mateyu 12:8. Werenganinso Marko 2:28.

Ndani analenga Sabata?

"Zonse zinalengedwa ndi Iye (Khristu, Mau)." Yohane 1:3.

Ndi tsiku lanji lomwe limadza pambuyo pa la Sabata?

"Ndipo popita dzuwa la Sabata, mbanda kucha, tsiku loyamba la sabata." Mateyu 28:1.

Dziwani ichi – Malingana ndi Chipangano Chatsopano, tsiku la Sabata linali litatha pamene limayamba tsiku loyamba la pa mulungu.

Kodi ndi tsiku liti la pa mulungu lomwe ndi la Sabata, "monga mwa lamulo"?

"Koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la 'Yehova' Mulungu wako." Eksodo 20:10.

Dziwani ichi – Kuti sitifunanso umboni wina ponena za Sabata m'Chipangano Chatsopano kuti ndi tsiku limodzomodzi monga liri ku Chipangano Chakale, palibe chinthu china chiri chonse chomwe chinachitika chakuti nkupangitsa tsiku'lo kusintha kuchoka pa la chisanu ndi chiwiri kupita pa loyamba la pa mulungu.

Kodi anthu opembedza Mulungu akufotokozedwa bwanji kuwalekanitsa ndi opembedza chirombo?

"Pano pali chipiriro cha oyera mtima, cha iwo akusunga malamulo a Mulungu ndi chikhulupiriro cha Yesu." Chibvumbulutso 14:12.

## Kusintha kwa Sabata

Kodi Sunday linayamba bwanji kuti lidzisungidwa ngati Sabata?

"Anthu ambiri amakhulupirira kuti Yesu anasintha Sabata, koma, kuchokera m'mau ake, zikuoneka kuti Iye analibe ganizo losintha'li ingakhale pang'ono. Choncho kusinthaku kukuyenera kuti kunachokera ku magwero ena.

M'chiphunzitso chake chotchuka cha pa Phiri chija, Khristu anati chiyani za chilamulo?

"Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri:sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa." Mateyu 5:17.

"Kufikira litapita thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo, kufikira zitachitidwa zonse." Mateyu 5:18.

Kodi Mulungu kudzera mwa mneneri Danieli anati ulamuliro wodziwika ndi dzina lakuti, "nyanga yaing'ono" udzayesa kuchita chiyani?

"Nidzanena mau akutsutsana ndi Wam'mwambamwamba, nidzalemetsa opatulika a Wam'mwambamwamba, nidzayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo." Danieli 7:25, RSV.

Nanga ndi ulamuliro uti womwe ukunena poyera kuti uli ndi mphamvu yakusintha malamulo a Mulungu?

Ulamuliro wa Papa.

Zinalembedwa motere – "Papa ali ndi ulamuliro waukuru ndi mphamvu zoti angathe ingakhale kusintha, kufotokoza, kapena kuti kumasulira malamulo a Mulungu...Papa angathe kusintha malamulo a Mulungu, chifukwa mphamvu zake si za umunthu, koma za Mulungu, ndipo iye ali nthumwi yokhayo yoimira Mulungu pa dziko lapansi." Zochokera mu Prompta Bibliotheca (Ready Library), "Papa," art., 2, lolembedwa ndi Lucius Ferraris.

Lamulo la Chinai

Ndi mpingo (wa Katolika) umene unasintha lamulo la chinai pochotsa Sabata monga mwa Mau a Mulungu, ndi kuika Sunday, kukhala lopumula." History of the Christian Church (1873), p.415, lolembedwa ndi N. Summerbell.

"Sunday, monga tsiku limene lapatulidwa mwapadera kukhala lopembedzera Mulungu Wamkurukuru, loyeretsedwa posagwira ntchito ya mtundu uli wonse ya dziko; kugula kapena kugulitsa, kapena zina ziri zonse za dziko ndipo polisunga ili monga lopembedza, ndi chinthu chimene mosabisa chinaikidwa ndi Mpingo wa Katolika." The American Catholic Quarterly Review, January, 1883, pp. 152, 139.

"Ngati amipingo ya mipanduko akadakhala kuti akutsatira Bukhu Lopatulika, mwenzi akupembedza Mulungu pa tsiku la Sabata. Posunga iwo Sunday akuchita lamulo la Mpingo wa Katolika." Yankho la Albert Smith, Chancellor of Achdiocese of Baltimore m'malo mwa Cardinal m'kalata yake ya pa February 10, 1920.

Kodi ndi ziphunzitso zotani zimene anthu azibweretsa m'malo mwa Mau a choonadi ndi amoyo?

"Anthu awa andilambira Ine kwachabe, ndi kuphunzitsa maphunzitso malangizo a anthu...Ndipo ananena nao, Bwino mukaniza lamulo la Mulungu, kuti musunge mwambo wanu." (Marko 7:7-9).

"Mukaikakaika kufikira liti? Ngati Yehova ndiye Mulungu, mtsateni Iye; ngati Baala, mumtsate iyeyo." 1 Mafumu 18:21.

Yesu anati, "Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu a mitundu yonse; ndipo pomwepo chidzafika chimariziro." Mateyu 24:14.

## Uthenga Wotsiriza wa Mulungu ku dziko la Uchimo.

Awerengi, m'kabuku aka mupitiriza kuwerenga za ndondomeko yachidule ndi yomveka ya Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu monga momwe walembedwera m'Bukhu Lopatulika wosasakaniza ndi miyambo kapena maphunzitso a umunthu.

"Ndi kunena ndi mau akuru, Opani Mulungu, mpatseni ulumelero; pakuti yafika nthawi ya chiweruziro chake." Chibvumbulutso 14:7.

Chiweruzo cha Mulungu chinayambira kumwamba m'chaka cha 1844. Chinayamba ndi akufa. Akufa sali kumwamba, iwo ali chigonere m'manda, kuyembekezera mdzukiro, "ena kunka ku moyo wosatha, ndi ena ku manyazi ndi mnyozo wosatha." Danieli 12:2.

Posachedwa, ingakhale palibe amene akudziwa, chiweruziro cha amoyo chiyamba.

"Mlambireni Iye amene analenga m'mwamba ndi mtunda ndi nyanja ndi akasupe amadzi." Chibvumbulutso 14:7.

Palibe munthu, papa, wansembe, kapena mlaliki angathe kukhululukira tchimo. Palibe munthu adzipembedzedwa. Yesu anati kwa iye, "Choka Satana, pakuti kwalembedwa, Ambuye Mulungu wako udzamgwadira, ndipo Iye yekha yekha udzamlambira." Mateyu 4:10.

Mariya, amai wa Yesu ali m'manda panopa. Sangathe kuthandiza munthu ali yense.

Yesu anati, "Ine ndi Atate ndife amodzi. Koma Ayuda anatolanso miyala kuti amponye Iye.

Yesu anayankha iwo, "Ndakuonetsani inu ntchito zabwino zambiri za kwa A tate; chifukwa cha ntchito yiti ya izo mundiponya miyala?

Ayuda anamyankha Iye, Chifukwa cha

ntchito yabwino sitikuponyani miyala, koma chifukwa cha mwano; ndi kuti Inu, muli munthu, mukudziyesera nokha Mulungu." Yohane 10:30-33.

"Ndidziwa mwano wa iwo akunena za iwo okha kuti ali Ayuda, osakhala Ayuda, komatu sunagoge wa Satana." Chibvumbulutso 2:9.

"Ndipo ananena ndi ine…pakuti nthawi yayandikira. Iye wakukhala wosalungama achitebe zosalungama; ndi munthu wonyansa akhalebe wonyansa….

"Taonani ndidza msanga; ndipo mphotho yanga ndiri nayo yakupatsa yense monga mwa ntchito yake…Kunja kuli agaru ndi anyanga, ndi chigololo…. ndi yense wakukonda bodza ndi kulichita." Chibvumbulutso 22:10-12,15.

"Ndipo anatsata mngelo wina mnzake ndi kunena, Wagwa, wagwa, Babulo." Chibvumbulutso 14:8.

## Kodi Babulo ndi ndani?

Bukhu la Chibvumbulutso limatenga maina ndi malo ndi zinthu zomwe zinalipo ndiponso kuchitika m'Chipangano Chakale ndi kuzigwiritsa ntchito mophiphiritsa m'Chipangano Chatsopano.

M'Chibvumbulutso Babulo akugwiritsidwa ntchito kuimira mipingo yonse yakugwa:

"Umene unamwetsako mitundu yonse ku vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake." Chibvumbulutso 14:8.

Belisazara mkati mwakuledzera anachitira mwano Mulungu.

"Anamwa vinyo, nalemekeza milungu yagolidi, ndi yasiliva, yamkuwa, yachitsulo, yamtengo, ndi yamwala." Danieli 5:4.

"Babulo wakhala chikho cha golidi m'dzanja la Yehova, amene analedzeretsa dziko lonse lapansi; amitundu amwa vinyo wake; chifukwa chake amitundu ali ndi misala." Yeremiya 51:7.

"Babulo akuimira DZIPEMBEDZO zonama, NDIPO VINYO AKUIMIRA ZIPHUNZITSO ZA DZIPEMBEDZO'ZO.

"Ndipo anadza mmodzi mwa angelo asanu ndi awiri akukhala nazo mbale zisanu ndi ziwiri nalankhula ndi ine, nanena, Idza kuno, ndidzakuonetsa chitsutso cha mkazi wachigololo wamkuru, wakukhala pa madzi ambiri (madzi ambiri ndiwo makamu, ndi mitundu ndi manenedwe Chibvumbulutso 17:15), amene mafumu a dziko anachita chigololo naye, ndipo iwo akukhala pa dziko analedzera ndi vinyo wa chigololo chake….

"Ndipo mkazi anabvala chibakuwa, ndi mlangali, nakometsedwa ndi golidi, ndi miyala ya mtengo wake, ndi ngale; nakhala nacho m'dzanja lake chikho chagolidi chodzala ndi zonyansa, ndi zodetsa za chigololo chake:

"Ndipo pamphumi pake padalembedwa dzina, CHINSINSI, BABULO WAUKURU, AMAI WA ACHIGOLOLO NDI WA ZONYANSITSA ZA DZIKO.

"Ndipo ndinaona mkazi woledzera ndi mwazi wa oyera mtima, ndi mwazi wa mboni za Yesu." Chibvumbulutso 17:1-6.

Mu ulauli MKAZI amaimira mbali zonse ziwiri za mpingo; wabwino kapena wopandukira.

Mkazi woipa (mpingo wabodza) umachedwa mkazi wachigololo. Werengani Chibvumbulutso 17:1.

Mkazi Wabwino (mpingo wachoonadi) umatchedwa namwali. Werengani Chibvumbulutso 14:4.

Mkazi woipa amachita chigololo ndi mafumu a dziko lapansi. Werengani Chibvumbulutso 17:2.

Mkazi wabwino ali mkwatibwi wa Khristu. 2 Akorinto 11:2.

Mkazi woipa wabvekedwa chibakuwa, ndi mlangali, nakometsedwa ndi golidi ndi miyala ya mtengo wake. Werengani Chibvumbulutso 17:4.

Mkazi wabwino wabvekedwa nsaru ya bafuta woyera woti mbu. Werengani Chibvumbulutso 19:8.

Mkazi woipa amaphunzitsa ziphunzitso za miyambo zomwe ndi zonyansa za chigololo chake. Werengani Chibvumbulutso17:4.

Mkazi wabwino amaphunzitsa Mau Oyera a Mulungu. Werengani Chibvumbulutso 14:5.

Mkazi woipa apangitsa malamulo oliumiriza dziko lapansi kuti litsatire malamulo a chipembedzo a umunthu. Werengani Chibvumbulutso 13:15.

Mkazi wabwino amasunga malamulo a Mulungu. Werengani Chibvumbulutso 14:12.

Mkazi woipa adzaononged wa ndi Mulungu. Werengani Chibvumbulutso 19:20.

Mkazi wabwino adzaima ndi Mulungu pa nyanja ya mandala. Werengani Chibvumbulutso 15:2..

"Ndinaona mngelo wina wakutsika m'Mwamba wakukhala nao ulamuliro waukuru; ndipo dziko linaunikiridwa ndi ulemelero wake.

"Ndipo anapfuula ndi mau olimba, nanena, Wagwa, wagwa, Babulo waukuru, nusandulika mokhalamo ziwanda, ndi mosungiramo mizimu yonse yonyansa, ndi mosungiramo mbalame zonse zonyansa ndi zodanidwa.

"Chifukwa ndi vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake mitundu yonse inagwa; ndipo mafumu a dziko anachita naye chigololo; ndipo ochita malonda a dziko analemera ndi mphamvu yakudyerera kwake.

"Ndipo ndinamva mau ena ochokera Kumwamba, nanena, Turukani m'menemo anthu anga; kuti mungayanjane ndi machimo ake, ndi kuti mungalandireko ya miliri yake." Chibvumbulutso 18:1-4. Kuturuka m'Babulo zitanthauza kuchoka m'mipingo yonama.

"Ndipo anawatsata mngelo wina, wachitatu, nanena ndi mau akuru, Ngati wina alambira chirombocho." Chibvumbulutso 14:9.

## Kodi Chirombo ndi ndani?

Mneneri Danieli anaona masomphenya, m'maloto momwe anaona "Zirombo zikuruzikuru zinai zosiyasiyana zikuturuka m'nyanja.

"Choyamba chinanga mkango." Danieli 7:3-4

BABULO, analamulira dziko lapansi kuchokera chaka cha 606 mpaka 539 BC.

"Chirombo china…chinanga chimbalangondo…chinatundumuka mbali imodzi." Danieli 7:5.

Gawo lina linali la mphamvu kuposa linzake. AMEDI NDI APEREZI, analamulira dziko lapansi kuchokera chaka cha 539 mpaka 331 BC.

Aperezi anali amphamvu, analamulira kumapeto.

"Pambuyo…china ngati nyalugwe." Danieli 7:6. AHELENE (GREECE) analamulira dziko lapansi kuchokera chaka cha 331 mpaka 168 BC.

"Pambuyo pake ndinaona chirombo cha chinai, choopsya ndi chochititsa mantha…chinali nao mano akuru achitsulo, chinalusa ndi kuphwanya ndi kupondereza chotsala ndi mapazi ake: chinasiyana ndi zirombo zonse zidachitsogolera; ndipo chinali ndi nyanga khumi." Danieli 7:7. ROMU WACHIKUNJA analamulira dziko lapansi kuchokera chaka cha 168 BC. Mpaka 538 AD.

"Anatero, chirombo chachinai ndicho ufumu wachinai pa dziko lapansi." Danieli 7:23.

Ufumu wa Romu wachikunja unagawika m'maufumu khumi pakati pa zaka za A.D. 351 ndi 476.

"Ndinali kulingirira za nyangazi, taonani, pakati pa izo panaphuka nyanga yina, ndiyo yaing'ono; patsogolo pake zitatu za nyanga zoyambazi zinazulidwa ndi mizu yomwe; ndipo taonani, m'nyanga m'menemo munali maso ngati maso a munthu, ndi pakamwa palikunena zazikuru." Danieli 7:8.

Kanyanga kakang'ono kameneka ndiko chirombo cha pa Chibvumbulutso 14:9. Ulamuliro wa UPAPA.

Ulamulirowu usanayambe kulamulira dziko lonse, unayamba wachita nkhondo ndi kuononga osakhalakonso maulamuliro atatu a khumi aja omwe ndi a Heruli, a Vandal ndi a Ostrogoth. Maufumu atatu a chi-Arian amenewa anaonongedwa osasiya ndi munthu mmodzi wambeu m'chaka cha AD 538 ndipo kuyambira chaka chimenechi Ulamuliro wa Upapa unakhala ndi mphamvu ingakhale pa maufumu ena onse a dziko lapansi kwa zaka 1,260, kuyambira AD 538-1798.

Onani kawerengedwe ka masiku m'munsimu:

"Ndinapenya, ndipo nyanga yomweyi inachita nkhondo ndi opatulikawo, niwalaka…Nidzanena mau akutsutsana ndi Wam'mwambamwamba, nidzalemetsa opatulika a Wam'mwambamwamba, nidzayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo; ndipo adzaperekedwa m'dzanja lake mpaka nthawi imodzi, ndi nthawi zina, ndi nthawi yanusu." Danieli 7:21-25.

"Ndipo mzinda wopatulika (mpingo woona) adzaupondereza miyezi makumi anai mphambu iwiri." Chibvumbulutso 11:2.

"Ndipo mkazi (mpingo woona) anathawira kuchipululu, kumene ali nayo mbuto yokonzekeratu ndi Mulungu, kuti kumeneko akamdyetse masiku chikwi chimodzi ndi mazana awiri mphambu makumi asanu ndi limodzi." Chibvumbulutso 12:6.

Mpingo woona unazunzidwa ndi mpingo wa Katolika kwa zaka 1,260, kuyambira chaka cha A.D. 538 mpaka 1798.

## Anthu Myandamyanda Anaphedwa

"Kunena kuti Mpingo wa Romu wakhesa mwazi wambiri wa anthu osalakwa kuposa bungwe liri lonse lakupha limene linakhalapo chilengdwere cha mtundu wa anthu, palibe munthu wochokera ku mipingo ya mipanduko wokhala ndi chidziwitso chokwanira cha mbiri ya dziko angatsutse. Palibe munthu angathe kunena mwatchutchutchu za kuchuruka kwa anthu amene anazunzidwa, ndiponso za kuzunzidwa kwao komwe kunali kwakukuru ndi koopsya kosowa nako mau akukufotokoza" W.E.H. Leeky, History of the Rise and influence of the Spirit of Rationalism in Europe. Vol.2:32, 1910 edition.

Zolembera zofotokoza momveka bwino ingakhale ziri zazitali kuwerenga, zonena kuti Mpingo wa Katolika unazunzadi, zikupezeka mu Catholic Encyclopedia, Vol. 12:266.

"Mbiri ya dziko ikufotokoza kuti, chifukwa chokhala ndi chikhulupiriro chosiyana ndi ziphunzitso za Mpingo wa Romu'wu, anthu ankhaninkhani kupyola (one hundred million) anaphedwa. Anthu a mtundu wa chi-Waldense ndi chi-Albigense (a Swiss ndi a French a chi-Protestant [Mpanduko]) anaphedwa pansi pa ulamuliro wa Papa Innocent III m'chaka cha

Malemba awa akutipatsa ife njira yomwe tingathe kumvetsetsera bwino za kawerengedwe ka nthawi – tsiku limodzi kukhala chaka chimodzi.

"Monga mwa kuwerenga kwa masiku amene munazonda dziko, masiku makumi anai, tsiku limodzi kuwerenga chaka chimodzi." Numeri 14:34.

"Ndakuikira masiku makumi anai, kuliyesa tsiku limodzi ngati chaka chimodzi." Ezekieli 4:6.

"Ndipo adzaperekedwa m'dzanja lake mpaka nthawi imodzi, ndi nthawi zina, ndi nthawi ya nusu." Danieli 7:25.

"Nthawi, ndi nthawi zina, ndi nthawi ya nusu." Chibvumbulutso 12:14.

Nthawi = chaka chimodzi.

Nthawi zina = zaka ziwiri.

Nthawi ya nusu = theka la chaka.

M'ulauli, chaka (nthawi) chimodzi = masiku 360.

Choncho nthawi 31/2 = 31/2x360 = masiku 1,260.

Tsono popeza tsiku limodzi liimira chaka chimodzi;

Masiku 1,260 = zaka 1,260.

1208. Kuyambira pamene bungwe la ma Jesuit linakhazikitsidwa mu zaka za 1540 mpaka 1580, anthu okwana zikwi mazana asanu ndi anai(900,000) anaphedwa. M'zaka makumi atatu, anthu okwana zikwi mazana khumi ndi asanu (150,000) anaphedwa pogwiritsa ntchito bwalo la zofufuzafufuza la milandu (Inquisition). M'zaka makumi atatu mphambu zisanu ndi zitatu (38) pansi pa lamulo loperekedwa ndi Charles V lolimbana ndi a Mipandukowo (Protestants), anthu zikwi makumi asanu anaphedwa ponyongedwa, kudulidwa mitu kapena kuponyedwa pa moto ali moyo ponena kuti anali oukira. Ena zikwi mazana khumi ndi asanu ndi atatu (153,000) anaphedwanso mu nthawi ya ulamuliro wa Mfumu Alva m'thawi ya zaka zisanu ndi theka." Brief Bible Readings, p.16.

John Wycliff, munthu wa Mulungu, anazunzidwa koopsya mu nthawi ya chizunzo cha ulamuliro wa apapa'chi, kufikira pakuti patapita zaka makumi anai kuchokera pomwe anaphedwa, mafupa ake anafukulidwa ndi kuotchedwa moto pamaso pa khwimbi la anthu. Ichi chidali chifukwa chakuti ndi zolembera za mtumiki wa Mulunguyu zomwe zidaonetsera poyera za ziphunzitso za bodza za Aroma.

Huss ndi Jerome anamangidwa ndi kuponyedwa pa moto a moyo. Chifukwa chakukanitsitsa kuleka kulalikira choonadi, ndipo ansembe a chikatolika anatsogolera anthu powaponya awiriwa ku malawi a moto. (Werengani Wylie, b3, ch. 17).

Ponena za Papa, a Martin Luther analemba, "Ndi chinthu chochititsa mantha kumuyang'ana munthu amene akudzitcha yekha kuti ali nthumwi yoimira Khristu, akukhala mu ulemelero woti palibe mfumu ndi imodzi yomwe inakhalapo motere. Kodi machitidwe amenewa ndi ofanana ndi a Yesu wosaukayo, kapenanso a Petro wodzichepetsayo? Iye (Papa), omtsatira ake, akuti ndi ambuye wa dziko lapansi! Koma Yesu amene Papayo akudzitcha kuti ali nthumwi yake, anati, 'Ufumu wanga si wa dziko lapansi ili.' Zingatheke bwanji kuti ulamuliro kapena kuti mphamvu za kazembe zipose za iye amene anamtuma kumuimira?" D'Aubigne, B, Ch. 3.

Luther anati, "Ndikukana ndi kutsutsana nacho [chikalata cha Papa (cholembedwa) kumnyoza Luther'yo] kuti ndi chosowa chilungamo ndi chabodza...Ndikukondwera kumva zowawa chifukwa cha choonadi. Ndipo panopa ndikumva kumasuka ndi mtendere mu mtima mwanga; chifukwa kuposa zonse ndazindikira kuti Papa ndi munthu wotsutsana ndi Khristu, ndikuti ulamuliro wake ndi ulamuliro wa Satana mwimi wake." D'Aubigne, B.6, Ch. 9.

## Kuyesa Kusintha Sabata

Ulamuliro wa Papa "udzayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo." Danieli 7:25. "Papa ali ndi mphamvu yaikuru yakuti angathe kusintha, kufotokoza, kapenanso kutanthauzira ingakhale malamulo a Mulungu. Papa angathe kusintha lamulo la Mulungu, chifukwa mphamvu zake si za munthu, koma za Mulungu, ndipo iye ali nthumwi yokhayo yoimira Mulungu pa dziko lapansi." Lucius Ferraris, Propta Bibliotheca, Popa art.2.

"N'zoonadi Mpingo wa Katolika umabvomereza kuti kusintha (kwa Sabata kukhala Sunday) kunachitidwa ndi iwo. Sizikadatheka kuti wina aliyense adzetse kusintha kwa za uzimu kapena za mpingo ndi za chipembedzo popanda iwo kutengapo mbali. Ndipo KUTERO NDI CHIZINDIKILO cha mphamvu zimene mpingowu uli nazo mu zinthu za chipembedzo." James Cardinal Gibbons mkalata yake yopita kwa J.F. Snyder wa ku Bloomington, ii. Nov, 11, 1895.

FUNSO – Kodi muli ndi njira ina yoti mungathe kutsimikizira kuti Mpingo uli ndi mphamvu kusintha zikondwerero za m'Malemba?

YANKHO – Ukadakhala kuti mpingo unalibe mphamvu zotere, sukadachita ichi chomwe ambiri achipembedzo a lero akubvomerezana nawo, sukadaika kusunga kwa Sunday, tsiku loyamba la pa sabata, m'malo mwa Saturday, tsiku lachisanu ndi chiwiri. Kusintha komwe nkosabvomerezeka kuchokera m'Malembo." Priest Stephen Keenan, A Doctrinal Catechism, Chap. 2, 174.

"Munditsimikizire ine kuchokera m'Bukhu Lopatulika zoti ine ndidzisunga Sunday kukhala lopatulika. Palibe lamulo lotere m'Bukhu Lopatulika! Ndi lamulo la Mpingo wa Katolika basi. Bukhu Lopatulika likuti, 'Uzikumbukila tsiku la Sabata likhale lopatulika.' Koma Mpingo wa Katolika umati, Ai! ndi mphamvu ya umulungu, ndikuthetsa tsiku la Sabata ndi kukuuzani kusunga tsiku loyamba la pa mulungu kukhala lopatulika. Ndipo zomvetsa chisoni! Dziko lonse la anthu ozindikira likugwada pansi kupereka ulemu pomvera lamulo la Mpingo Woyera wa Katolika." Priest Thomas Enright, C.S.S.R, president of Redemptorist College, Kansas City, M0 in a lecture at Hartfold, Kansas, Feb. 18, 1884, and in the American Sentinel, a Roman Catholic journal of June 1893, 173.

Palibe munthu angasinthe lamulo loyera la Mulungu, koma angathe kungoyesa kutero.

Yesu anati, "Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri: sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa. Pakuti indetu ndinena kwa inu, Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo, kufikira zitachitidwa zonse." Mateyu 5:17-18.

Paulo akuti, "Munthu asakunyengeni konseko: kuti silifika, koma chiyambe chifike chipatukocho, nabvumbulutsidwe munthu wosayeruzika, mwana wa chionongeko;

"Amene atsutsana nazo, nadzikuza pa zonse zotchedwa Mulungu, kapena zopembedzeka; kotero kuti iye wakhala pansi ku Kachisi wa Mulungu, nadzionetsera yekha kuti ali Mulungu." 2 Atesalonika 2:3-4.

"Papa ndi munthu wa ulemu wake waukuru ndipo wakwezedwa kufikira poti sali munthu wamba, koma Mulungu, ndi nthumwi ya Mulungu. Potengera ndi udindo woposa wotere akutchedwa m'episkopi wa a episkopi. Choncho ali ngati mfumu ya ulemelero woposa mafumu onse, ndi Mfumu ya mafumu. Ichi n'chifukwa chake amabvekedwa nduwira yokhala ndi akorona atatu, monga Mfumu ya kumwamba ndi ya dziko lapansi ndiponso ya kumaiko a kunsi kwa dziko." Lucius Ferraris, Prompta Bibliotixeca, Vol 6, p 29.

"Ndipo umodzi wa mitu yake unakhala ngati unalasidwa kufikira imfa." Chibvumbulutso 13:3.

":Ngati munthu alinga ku ndende, kundende adzamuka; munthu akapha ndi lupanga, ayenera iye kuphedwa nalo lupanga." Chibvumbulutso 13:10.

Tafotokoza kale kuti ulamuliro wa papa unachitika pa dziko kwa zaka 1,260 – A.D. 538-1798. Werengani pa chati chija.

Mu 1798 Ulamuliro wa nkhanza ndi Kupha unapitirira kudzera mu kuukira kofuna kusintha zinthu komwe kunachitika kotchedwa French Revolution koma chipembedzo cha Chikatolika mu France sichinakhuzidwe. Koma a nkhondo a chi-French pansi pa utsogoleri wa Berthier, analowa m'Romu namtenga undende papa. Izi zinachitika pa Feb. 10, 1798. Papa wotengedwa undendeyo anafera m'ndende m'Valance, France m'chaka chotsatira. Zitachitika izi kunamveka kupfuula, "Chikatolika chafa." Ulamuliro wa ufumu wa a Papa unalandira "bala la ku imfa." Werengani Chibvumbulutso 13:3. Koma tikuuzidwa kuti bala la kuimfa'lo lidapola, ndipo posachedwa dziko lonse lapansi lidzazizwa "potsata chirombocho." Ibid.

Mu 1929 Cardinal Gasparre anakomana ndi Mussolini ku nyumba ya chifumu ku St. John Lateran komwe Pangano la Vatikani lobwezera mphamvu za ulamuliro kwa Papa linasainidwa ndipo Vatikani anakhalanso dziko ndi ufumu woima pa wokha.

Koma bala lakuimfa lija silinapoleretu ai.

Bala la kuimfa'li linali kulekana komwe kunachitika pakati pa mpingo wa Romu ndi ulamuliro wake za dziko; ndipo pamene ili lidzapola kotheratu, Mpingo wa Katolika udzayamba kulamuliranso mabwalo a milandu a dziko lapansi. Dziko la Amerika lidzakhala mtumiki wodzetsa kupola kwa bala'lo:

"Ndipo ndinaona chirombo china chirinkuturuka pansi; ndipo chinali nazo nyanga ziwiri ngati za mwa wa nkhosa, ndipo chinalankhula ngati chinjoka.

"Ndipo chichita ulamuliro wonse wa chirombo choyamba pamaso pake. Ndipo chilambiritsa dziko ndi iwo akukhala momwemo chirombo choyamba, chimene bala lake la kuimfa lidapola." Chibvumbulutso 13:11-12.

## Chizindikilo cha Chirombo

"Ngati wina alambira chirombocho, ndi fano lake, nalandira lemba pamphumi pake, kapena pa dzanja lake, iyenso adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu, wokonzeka wosasanganiza m'chikho cha mkwiyo wake; ndipo adzazunzika ndi moto ndi sulfure pamaso pa angelo oyera mtima ndi pamaso pa Mwanawankhosa." Chibvumbulutso 14:9-10.

CHIZINDIKILO CHA CHIROMBO NDI CHIPEMBEDZO CHA SUNDAY chomwe chidzakakamizidwa mwa lamulo – Chomwenso ndi chizindikilo cha Mpingo wa Katolika.

Mpingo wa Katolika ukubvomereza

kuti, "Nzoonadi Mpingo wa Katolika ukubvomera za kusintha (Sabata kukhala Sunday) kuti unakuchitadi…Ndipo ichi ndi CHIZINDIKILO chosonyeza mphamvu ya umulungu wake." Cardinal Gibbons, Nov. 11, 1895.

Posachedwapa dziko la Amerika libwezera mphamvu za ulamuliro wa za ndale ku ulamuliro wa Upapa.

"Ndipo chisokeretsa iwo akukhala padziko ndi zizindikilo zimene anachipatsa mphamvu yakuzichita pamaso pa chirombo, ndi kunena kwa iwo akukhala padziko, kuti apange fano la chirombo, chimene chinali nalo bala la lupanga nichinakhalanso ndi moyo.

"Ndipo anachipatsa mphamvu yakupatsa fano la chirombo mpweya, kutinso fano la chirombo lilankhule, nilichite kuti onse osalilambira fano la chirombo aphedwe.

"Ndipo chichita kuti onse, ang'ono ndi akuru, achuma ndi osauka, ndi mfulu ndi akapolo, alandire chilembo pa dzanja lao ndi pamphumi pao;

"Ndi kuti munthu sangakhoze kugula kapena kugulitsa, koma iye yekha wakukhala nacho chilembo, ndilo dzina la chirombo, kapena chiwerengero cha dzina lake." Chibvumbulutso 13:14-18.

Dziko la Amerika linaturuka pansi pa dziko kukhala mtundu waukuru mwakachetechete m'zaka za m'ma 1798 m'nthawi yokhayokhayo yomwe ulamuliro wa Upapa umapita kumapeto. Mtundu waukuru wa Amerika'wu ukuimiridwa ndi nyanga ziwiri ngati za mwana wa nkhosa – mtundu wopanda mfumu ndi mpingo wopanda Papa. Mtundu umene wakhala ukudziyamikira za ufulu wa chipembedzo ndiponso ulamuliro wokomera anthu onse wa demokolase momwe nzika iri yonse imatengako mbali pakayendetsedwe ka boma. Koma chomvetsa chisoni mtundu waukuru'wu posachedwa ulankhula ngati CHINJOKA.

> "Njira yopambana yakumlemekezera Papa Yohane Paulo Wachiwiri, m'modzi wa amuna otchuka, ndiyo kutsatira ziphunzitso zake ndi mtima wonse; kumvera mau ake ndikuwaika m'ziphunzitso zakezo ndi m'machitachita muno mu Amerika. Uku ndikubetchela kwakukuru komwe tiyenera kukulandira." President George W. Bush; March 21, 2001.
>
> Pakunena za kumangidwa kwa malo a za chikhalidwe a Pope John Paul Cultural Center m' Washington, D.C. Papa anati, "Tikhala tikubwera kudzaona malo ano ngati ka Vatikani kakang'ono mu Amerika." Monga zinafotokozedwera ndi Paul Shepard wolemba wa AP. The Daily News, March 24,2001.

Malamulo a dziko la Amerika amati, "Nyumba ya malamulo sidzapanga lamulo lokhuza za kakhazikitsidwe ka zipembedzo, kapena kuletsa zoterozo; kapena kusokoneza ufulu wolankhula za kukhosi, kapena wa zofalitsafalitsa; kapena ufulu wa anthu wakusonkhana, ndiponso kuletsa anthu kulifikira Boma pa zobvuta zao."

Abraham Loncoln polankhula ku Gettysburg analitcha boma la Amerika, "Boma la anthu, lopangidwa ndi anthu,ndi kuyendetsedwa ndi anthu."

Anthu a ku Amerika anapanga Malamulo omwe amalimbikitsa ufulu wachipembedzo kwa anthu onse. Anthu a ku Amerika omwewo posachedwapa kudzera poponya maere, oumiriza nyumba yao ya malamulo kuti isinthe Malamulo ake. Bukhu Lopatulika likutiuza kuti kudzera mwa mizimu ya ziwanda dziko lonse lapansi lidzasokeretsedwa. Padzakhala anamondwe, zibvomezi, njala, miliri ndi matenda. Nthawi ikamayandikitsitsa ku mapeto zochitikazi zidzapitirira kuipiraipira, ndipo anthu a Mulungu adzanamiziridwa kuti ndiwo akudzetsa izi. Atumiki a chipembedzo cha Satana ndi alaliki ambiri adzanena kuti zoopsya'zi sizingathe mpaka Sunday litalemekezedwa ndi anthu onse.

Anthu adzafuna malamulo a Sunday. Dziko la Amerika lidzatsogolera ndipo dziko lonse lapansi lidzatsatira. "Ndipo dziko lonse linazizwa potsata chirombocho." Chibvumbulutso 13:3.

"Ndipo chisokeretsa iwo akukhala padziko ndi zizindikilo zimene anachipatsa mphamvu yakuzichita pamaso pa chirombo, ndi kunena kwa iwo akukhala padziko. Kuti apange fano la chirombo, chimene chinali nalo bala la lupanga nichikhalanso ndi moyo." Chibvumbulutso 13:14.

"Ndipo ndinaona moturuka m'kamwa mwa chinjoka, ndi m'kamwa mwa chirombo, ndi m'kamwa mwa mneneri wonyenga mizimu itatu yonyansa ngati achule; pakuti ali mizimu ya ziwanda zakuchita zizindikilo; zimene zituruka kumka kwa mafumu a dziko lonse, kuwasonkhanitsira ku nkhondo ya tsiku lalikuru la Mulungu, Wamphamvuyonse." Chibvumbulutso 16:13-14.

"Koma Mzimu anena monenetsa, kuti m'masiku otsiriza ena adzataya chikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosokeretsa ndi maphunziro a ziwanda, m'maonekedwe onyenga a iwo onena mabodza, olochedwa m'chikumbu mtima mwao monga ndi chitsulo cha moto." 1 Timoteo 4:1-2.

Onse amene adzakane kumvera lamulo ili adzaopsyezedwa kuti alipire, komanso pomangidwa ndiponso kuphedwa kumene.

"Ndipo anachipatsa mphamvu yakupatsa fano la chirombo mpweya, kutinso fano la chirombo lilankhule, nilichite kuti onse osalilambira fano la chirombo aphedwe." Chibvumbulutso 13:15.

Malamulo awa a Sunday adzabvomerezedwa ku Amerika, kenaka dziko liri lonse lidzatsatira – Old Mexico, South America, India, Asia, Europe, Russia, Africa ndi zisumbu zonse za m'nyanja. Munthu ali yense m'dziko lapansi adzayenera kupanga chisankho, kumvera lamulo la Mulungu kapena lamulo la munthu.

"Ndipo adzachilambira (chirombo) onse akukhala padziko, amene dzina lao silinalembedwa m'bukhu la moyo la Mwanawankhosa, wophedwa kuyambira makhazikitsidwe a dziko lapansi." Chibvumbulutso 13:8.

"Ndipo utsi wakuzunza kwao ukwera ku nthawi za nthawi; ndipo sapuma usana ndi usiku iwo akulambira chirombocho ndi fano lake, ndi iye ali yense akalandira lemba la dzina lake." Chibvumbulutso 14:11.

Tingathe kufunsa funso: Zinachitika bwanji kuti Romu wa pansi pa ulamuliro wa Papa akhale wa mphamvu zochuruka chotere?

"Ndipo ndinaimirira pa mchenga wa nyanja, ndipo ndinaona chirombo (Romu Wachikunja) chirinkuturuka m'nyanja, chakukhala nazo nyanga khumi, ndi mitu isanu ndi iwiri… ndi pamitu pake maina a mwano.

"Ndipo chirombo (Romu pansi pa ulamuliro wa Papa) ndinachionacho chinafanana ndi nyalugwe, ndi mapazi

Ziphunzitso ndi miyambo za Mpingo wa Katolika Zotsutsana ndi Baibulo ndi chaka chimene chiphunzitso chiri chonse chinayamba:

A.D. 300: Kupempherera akufa ndi chizindikilo cha mtanda
321: Malamulo okakamiza kusunga Sunday.
375: Kulemekeza angelo ndi anthu oyera mtima omwe anafa kale ndi kugwiritsa ntchito mafano.
394: Chiyambi cha Ukaristiya wachikunja.
400: Kuzunzidwa kwa anthu omwe anasunga Sabata loona la m'Bukhu Lopatulika.
431: Chiyambi chokweza ndi kupembedza Mariya monga "Amai wa Mulungu."
450: Chilango cha imfa kwa iwo osunga Sabata la m'Bukhu Lopatulika.
500: Ansembe anayamba kubvala modzilekanitsa ndi anthu ena.
526: Chikhulukiro cha machimo polapa kwa anzathu
593: Chiphunzitso cha limbo.
600: Kupembedza m'chi- Latin chokhachokha, kuyamba kwa mapemphero odzera mwa Mariya, angelo ndi oyera mtima omwe anafa kale.
607: Episkopi wa Mpingo wa Romu atchedwa Papa Kapena kuti Mtsogoleri wa Mpingo wa pa malo ponse.
709: Kumpsyopsyona phazi la Papa.
750: Pokhala mtsogoleri wa Mpingo, Papa akhalanso mtsogoleri wa za dziko.
786: Kugwadira mtanda, mafano, zithunzi ndi mafupa.
927: Kukhazikitsidwa kwa bungwe la a Episkopi (College of Cardinals).
965: Kubatiza mabelu.
995: Kusankha akufa ena kuti ndi oyera mtima.
998: Kusala kudya tsiku la Friday ndi nthawi ya masautso a Yesu.
1079: Kusakwatira kwa ansembe.
1090: Kukhazikitsidwa kwa Rosary ndi mapemphero ogwiritsa ntchito mikanda.
1184: Kukhazikitsidwa kwa bwalo la milandu lolangira oukira Mpingo.
1190: Kugulitsa kwa dzikalata zachikhululukiro.
1215: Kulapa kwa machimo kwa ansembe m'malo mwa kwa Mulungu.
1220: Kuyamba kudalitsa madzi.
1229: Kuletsedwa kwa Bukhu Lopatulika kuti lisawerengedwe ndi akhristu wamba.
1251: Kukhululukira uchimo mwa umunthu.
1414: Kuletsedwa kwa chikho cha mgonero kwa anthu.
1508: Ave Mariya kunenedwa pamodzi ndi mikanda.
1524: Kukhazikitsidwa kwa bungwe la ma Jezwiti.
1545: Miyambo ndi ziphunzitso za chikatolika kuti zofanana ndi mphamvu ndi Mau a Mulungu.
1546: Mabukhu a Apokurafa aikidwa m'Bukhu Lopatulika.
1854: Chiphunzitso cha Mariya Wopanda chirema chiri chonse cha uchimo
1864: Kuletsa kwa ufulu wachipembedzo, kulankhula, kusankha, kufalitsa, ndi wa zofufuzafufuza za sayansi kuti zonsezo ndi kuchimwa.
1870: Kuti Papa sachimwa.
1930: Sukulu zonse za boma ndi zina zonse zosakhala za chikatolika zinaletsedwa.
1950: Kukweza Mariya.
1965: Chikhulupiriro chakuti Mariya ndi amai wa mpingo ndi zina monga kusakwatira kapena kusakwatiwa, kusankha undekha, kumanga malo a za chipembedzo, nthawi ya mazunzo a Yesu, mlungu woyera, La Sunday la Kanjedza, Madzi oyera, lachitatu la phulusa, la Oyera onse, chikhulupiriro cha mizimu ya akufa, tsiku la kachidutswa ka mnofu wa nsomba, kukwapula wochimwa zikwapu monga chilango, kufukiza lubano, mafuta oyera, nyota, matsenga, etc.

ake ngati mapazi a fisi, ndi pakamwa pake ngati pakamwa pa mkango; ndipo chinjoka (Romu Wachikunja) chinampatsa iye(Romu pansi pa ulamuliro wa Papa) mphamvu yake, ndi mpando wachifumu wake, ndi ulamuliro waukuru…Ndipo dziko lonse linazizwa potsata chirombocho (Romu pansi pa ulamuliro wa Papa)." Chibvumbulutso 13:1-3.

"Kuchotsa kwa likuru la ufumu ku Romu kupita ku Constantinople mu A.D.330 kunapereka mpata ku Mpingo wa Kumadzulo kukhala womasuka kuchoka mu ulamuliro wa mfumu, ndi kuyamba kulinganiza kayendetsedwe kake pawokha. M'Episikopi wa Romu, pokhala m'malo omwe anali a mafumu anakhala munthu wamkuru Kumadzuloko, nakakamizika kukhala mtsogoleri wa za ndale komanso wa za uzimu." A.C. Flick, The Rise of the Medieval Church, p. 168.

"Ingakhale panali zobvuta zina za chi-Roma anthu a chi-babarian ndi a chi Aryan anakhala….pansi pa chitchinjirizo cha Episkopi wa Romu, yemwe analinso ndi mphamvu pambuyo pakuchoka kwa mfumu…Mpingo wa Romu unapezerapo mwai wakukwera ndi kutenga ulamuliro, nupanga Ufumu wa Aroma wa dziko lonse lapansi, komwe kunangokhala kupitiriza ufumu womwe unalipo kale; kutanthauza kuti sikudali kutha kwa ufumu woyambawo, koma kungosintha kachitidwe. Iwo [Mpingo wa Katolika] unapangidwa kudzera mu ndale, ndipo umadzionetsera kuti uli ufumu wa dzko lonse lapansi, chifukwa uli gawo la ufumu wa Romu Wachikunja. Papa, yemwe amadzitcha Mfumu ndiponso Pontifex Maximus, ndi mlowa m'malo wa Kaisara" Adolf Hamock, What is Christianity? 1903, pp. 269-270.

Mu mpingo uli wonse muli akhristu oona, ingakhale iwo opembedza tsiku la Sunday, kuphatikiza a mu Mpingo wa Katolika. Iwo akuchita zinthu pogwiritsa ntchito kuunika komwe ali nako. Akutumikira Mulungu ndi mtima wao wonse kudzera m'chidziwitso chomwe achilandira. Ingakhale akusunga Sunday, sanafike polandira CHIZINDIKILO CHA CHIROMBO ai. Koma kuyambira pamene SUNDAY lidzakhala lokakamizidwa mwa lamulo. Munthu ali yense wodzalisunga adzalandira chizindikilo cha chirombo. Ili ndi gulu la anthu omwe adzalangidwa ndi miliri isanu ndi iwiri:

"Ndipo anachoka woyamba, natsanulira mbale yake kudziko; ndipo kunakhala chironda choipa ndi chosautsa pa anthu akukhala nalo lemba la chirombo nalambira fano lake." Chibvumbulutso 16:2.

## Chizindikilo cha Mulungu

Si anthu onse omwe adzalandira Chizindikilo cha Chirombo:

"Ndipo ndinaona ngati nyanja ya mandala, yosanganiza ndi moto; ndipo iwo amene anachilaka chirombo, ndi fano lake ndi chiwerengero cha dzina lake, anaimirira pa nyanja ya mandala, nakhala nao azeze a Mulungu." Chibvumbulutso 15:2.

Iwo amene sadzalandira Chizindikilo cha Chirombo, adzalandira Chizindikilo cha Mulungu.

"Nanena, Musaipse dziko, kapena nyanja, kapena mitengo kufikira tidasindikiza chizindikilo akapolo a Mulungu wathu, pamphumi pao." Chibvumbulutso 7:3.

"Manga umboni, mata chizindikilo pachilamulo mwa aphunzi anga." Yesaya 8:16.

Pachizindikilo cha Mulungu pali DZINA, UDINDO, NDIPONSO MALO omwe lamulo likugwiritsidwirako ntchito:

"Udzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza ntchito zako zonse; koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire ntchito iri yonse, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wamwamuna, kapena mwana wako wamkazi, kapena wantchito wako wamwamuna, kapena wantchito wako wamkazi, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali m'mudzi mwako;

"chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika." Eksodo 20:8-11.

"Ndicho chizindikilo chosatha pakati pa Ine ndi ana a Israyeli; pakuti Yehova analenga zam'mwamba ndi dziko lapansi masiku asanu ndi limodzi, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri, naonanso mphamvu." Eksodo 31:17.

"Muzipatulanso masabata anga, ndipo adzakhala chizindikilo pakati pa Ine ndi inu, kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu." Ezekieli 20:20.

Tsiku la Sabata la chisanu ndi chiwiri liri chikhalire tsiku lopatulika la Yehova ndipo kusunga lamulo ili kudzakhala yeso lotsiriza ponena za CHIZINDIKILO CHA MULUNGU.

"Ndipo ndinaona mngelo wina, anakwera kuchokera poturuka dzuwa, ali nacho chizindikilo cha Mulungu wamoyo… nanena, musaipse dziko kapena nyanja, kapena mitengo, kufikira tidasindikiza chizindikilo akapolo a Mulungu wathu, pamphumi pao." Chibvumbulutso 7:2-3.

"Pakuti monga m'mwamba mwatsopano ndi dziko lapansi latsopano limene ndidzalenga, lidzakhalabe pamaso pa Ine, ati Yehova, momwemo adzakhalabe ana anu ndi dzina lanu.

"Ndipo kudzakhala kuti kuyambira pa mwezi wokhala kufikira ku unzake, ndi kuyambira pa Sabata lina kufikira ku linzake, anthu onse adzafika kudzapembedza pamaso pa Ine, ati Yehova." Yesaya 66:22-23.

"Ndinagwidwa ndi Mzimu tsiku la Ambuye." Chibvumbulutso 1:10.

## Kodi tsiku la Ambye ndi liti?

"Ndipo Iye ananena kwa iwo, kuti, Mwana wa munthu ali Mbuye wa tsiku la Sabata." Luka 6:5.

Tsiku la Ambuye ndi la Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri la pa mulungu.

Lamulo la Sunday likufotokozedwa kuti liri nkhondo yolimbana ndi anthu a Mulungu za Sabata loona.

"Ndipo chinjoka chinakwiya ndi mkazi, nichinachoka kunka kuchita nkhondo ndi otsala a mbeu yake, amene asunga malamulo a Mulungu, nakhala nao umboni wa Yesu." Chibvumbulutso 12:17.

"Odala iwo amene atsuka miinjiro yao, kuti akakhale nao ulamuliro pa mtengo wa moyo, ndi kuti akalowe m'mzinda pazipata." Chibvumbulutso 22:14.

Mipingo yochuruka kudzanso zipembedzo, sakusunga malamulo koyenera ai. Iwo amasakaniza choonadi ndi chikunja, miyambo ya anthu.

"Koma andilambira Ine kwachabe, ndi kuphunzitsa maphunzitso malangizo a anthu." Mateyu 15:9.

Kusunga sabata la Sunday ndi mwambo wa anthu kuchokera ku chipembedzo cha chikunja cha dzuwa. Kunena kuti munthu akafa amakhala ali moyo kumwamba sichiphunzitso chochokera m'Bukhu Lopatulika. Kubatiza ana ang'ono komanso ubatizo wowaza madzi sizikuchokeranso m'Bukhu Lopatulika.

"Ife Akatolika, tiri ndi ufulu wakusunga Sunday monga tsiku lopatulika, m'malo mwa Saturday, monga momwe tikuphunzitsidwira m'miyambo ya Mpingo. Pamene inu a Mipanduko (Protestants) mulibe ulamuliro uli wonse; pakuti palibe pomwe Bukhu Lopatulika likukuuzani kulisunga (Sunday), ndipo simungabvomereze kuti pangakhalenso wina wokuuzani kutero kuchokera kwina kulikonse. Mosabisa, tonse inu ndi ife, tikutsatira miyambo pa nkhani'yi; koma tikutsatira pokhulupirira kuti ili mbali ya Mau a Mulungu, ndipo Mpingo (wa Katolika) unapatsidwa mphamvu ya umulungu yakutanthauzira mau'wo; inu mukutsatira za Mpingo wa Katolika'wo, koma nkumaunyoza nthawi zonse kuti ndi wakugwa ndi wosokeretsa, chomwe chikupangitsa kuti malamulo a Mulungu'wa asamagwire ntchito yao koyenera." [Zochokera pa Mateyu 15:6]. The Brotherhood of St. Paul, "The Cliflon Tracts" Vol 4, Tract 4, p. 15.

"Ndafuna ndiwakumbutse a Presbyterian, Baptist, Mthodist ndi akhristu ena onse, kuti palibe pena paliponse pomwe Bukhu Lopatulika likuwabvomereza kusunga Sunday. Sunday ndi lokhazikitsidwa ndi Mpingo wa Katolika, ndipo iwo amene akusunga tsiku'li akusunga lamulo la Mpingo wa Katolika." Priest Brody, mau ake analankhula ndi kufalitsidwa m'Elizabeth, N.J. News ya March 18, 1903.

### A MPANDUKO ABVOMEREZA

Abusa, anthu ophunzira, ndi olemba otchuka, ambiri a iwo mosakaika konse osunga Sunday monga mwa mwambo wa mpingo: koma mosabisa konse akuchitira umboni kuti Sabata la m'Bukhu Lopatulika ndi tsiku lachisanu ndi chiwiri la pa mulungu, [Saturday] osati Sunday. Sunday si tsiku la Ambuye.

### AMIPANDUKO ALANKHULAPO

Mpingo wa Congregationalist: Ndi zodziwika bwino kuti ingakhale ife tiumirere kusunga Sunday ngati tsiku lopembedza, sitikusunga Sabata…Sabata linakhazikitsidwa mwapadera ndi chifuniro cha Mulungu. Choncho sitingathe ife kuliyerekeza ili ndi Sunday…Palibe ndi lemba ndi limodzi lomwe m'Chipangano Chatsopano lomwe likutiuza kuti tidzalangidwa ngati sitingasunge Sunday kukhala lopatulika." Dr. R. W. Dale, "The Ten Commandments," pp. 106-107.

Mpingo wa Free Lutheran: "Chifukwa chakusowa umboni wochokera pena paliponse m'Bukhu Lopatulika wotsimikiza kuti mwina Ambuye mwini wake kapena atumwi analamulira za kusintha kwa Sabata kukhala Sunday, sichapafupi kuyankha funso lakuti: Ndi ndani anasintha Sabata, ndiponso ndi ndani anali ndi ulamuliro wakutero?" George Sverdrup, "A New Day."

Mpingo wa Presbyterian: "Palibe liu, palibe ganizo m'Chipangano Chatsopano lonena kuti munthu asagwire ntchito pa Sunday. Kusunga lachitatu la phulusa ndi nthawi ya kukumbukira mazunzo a Yesu ziri ndi magwero amodzi ndi kusunga Sunday. Lamulo la Mulungu silinenapo chiri chonse za sabata la Sunday." Canod Eyton, mu "the Commandments."

Mpingo wa Anglican: "Ndi pati m'Bukhu Lopatulika pomwe pakutiuza kuti tidzisunga tsiku loyamba la pa mulungu? Tikuuzidwa kusunga tsiku lachisanu ndi chiwiri; koma sitikuuzidwa kusunga tsiku loyamba la pa mulungu." Isaac Williams, "Plain Sermons on the Catechism," pp. 334, 336.

Mpingo wa Methodist: "Ndi zoona kuti palibe lamulo lonena za ubatizo wa ana ang'ono. Palibenso ndi limodzi lomwe lonena za kusunga tsiku loyamba la pa mulungu kukhala lopatulika. Ambiri amaganiza kuti Khristu ndiye anasintha Sabata. Koma kuchokera m'mau a pa kamwa pake, zikupezeka sanadze Iye kudzachita ichi. Iwo amene amakhulupirira kuti Yesu anasintha Sabata akuchita ichi pongoganiza." Amos Binney, Theological Compendiun, pp. 180-181.

Mpingo wa Episcopalian: "Tasintha kuchoka pa tsiku lachisanu ndi chiwiri kupita ku tsiku loyamba la pa mulungu, kuchoka Saturday kupita Sunday, pomvera ulamuliro wa mpingo umodzi woyera wa Khristu wa atumwi wa Katolika." Bishop Seymour, "Why Keep Sunday."

Mpingo wa Baptist: "Ndikudziwa ndithu kuti Sunday silinagwiritsidwa ntchito monga tsiku la kupembedzo mu Mbiri ya akhristu woyambawo, monga momwe tikuphunzirira kuchokera kwa Atsogoleri a chikhristu oyambirirawo ndiponso zolembera zina. Koma chomvetsa chisoni kuti tsiku'li likunenedwa kuti liri chizindikilo cha Chikunja, komanso kutchedwa kuti ndi tsiku la mulungu wa dzuwa, lomwe linasankhidwa ndi kupatulidwa ndi kupandukira Mulungu kwa Papa, koma nkumasungidwanso ngati lopatulika ndi a Mipanduko." Dr. E.T. Hiscox, report of his Sermon at the Baptist Ministers Convention, in New York Examiner, November 16, 1893.

Talemba motalikirapo pogwiritsa ntchito maumboni a Akatolika omwe akunena mwatchutchutchutchu kuti ndiwo anasintha Sabata kuchoka pa Saturday, tsiku la chisanu ndi chiwiri la pa mulungu kupita ku Sunday, tsiku loyamba la pa mulungu. Akutsimikizira kuti ndi iwo anabweretsa chipembedzo cha Sunday mu Mpingo wa Chikhristu kuti anthu onse adzisunga tsiku la chipembedzocho.

Talembanso pogwiritsa maumboni a abusa ndiponso alembi otchuka ochokera ku mipingo ya Mpanduko, omwe afotokozanso mosabisa mau kuti palibedi lemba ndi limodzi m'zipangano zonse Chakale kapena Chipangano Chatsopano pomwe pakuchitira umboni za chipembedzo cha Sunday kapena za kupatulika kwa tsiku'li.

Sunday si tsiku lopatulika. Sunday monga tsiku lopembedza linachokera kuchipembedzo cha chikunja cha dzuwa.

"Inunso mulumphiranji lamulo la Mulungu chifukwa cha miyambo yanu?.... Onyenga inu! Yesaya ananenera bwino za inu, ndi kuti, Anthu awa andilemekeza Ine ndi milomo yao; koma mtima wao uli kutari ndi Ine. Koma andilambira Ine kwachabe, ndi kuphunzitsa maphunzitso, malangizo a anthu….

"M'mera uliwonse umene Atate wa Kumwamba sanaubzala, udzazulidwa. Kawalekeni iwo, ali atsogoleri akhungu. Ndipo ngati wakhungu amtsogolera wakhungu, onse awiri adzagwa m'mbuna." Mateyu 15:3, 7-9, 13-14.

Chenjezo lotsiriza lotsutsana ndi chizindikilo cha chirombo lidzakhala Uthenga wa paliponse pa dziko lapansi. Udzalalikidwa m'nyumba za mphepo, za akanema ndi m'mapepala ofalisa nkhani m'dziko liri lonse lokhala pa nkhope ya dziko lapansi. Mulungu adzapereka mpata kwa munthu ali yense wakusankha, kumvera Iye, kapena kumvera malamulo opangidwa ndi munthu omwe ndi otsutsana mwachindunji ndi malamulo a Mulunguyo.

"Zitatha izi ndinaona mngelo wina wakutsika m'Mwamba wakukhala nao ulamuliro waukuru; ndipo dziko lapansi linaunikiridwa ndi ulemelero wake.

"Ndipo anapfuula ndi mau olimba, nanena, Wagwa, wagwa, Babulo waukuru, nusandulika mokhalamo ziwanda, ndi mosungiramo mizimu yonse yonyansa, ndi mosungiramo mbalame zonse zonyansa ndi zodanidwa.

"Chifukwa ndi vinyo wa mkwiyo wa chigololo chake mitundu yonse idagwa; ndipo mafumu a dziko anachita naye chigololo; ndipo ochita malonda a dziko analemera ndi mphamvu ya kudyerera kwake.

"Ndipo ndinamva mau ena ochokera Kumwamba, nanena, Turukani m'menemo anthu anga; kuti mungayanjane ndi machimo ake, ndi kuti mungalandireko ya miliri yake.

"Pakuti machimo ake anaunjikizana kufikira m'Mwamba, ndipo Mulungu anakumbukira zosalungama zake.

"Muubwezere, monganso uwu unabwezera, ndipo muwirikize kawiri monga mwa ntchito zake; m'chikhomo unathiramo, muuthirire chowirikiza.

"Chifukwa chake miliri yake idzadza m'tsiku limodzi, imfa, ndi maliro, ndi njala; ndipo udzapserera ndi moto; chifukwa Ambuye Mulungu wouweruza ndiye wolimba." Chibvumbulutso 18:1-6, 8.

"Ndipo mafumu a dziko, ndi akuru, ndi akazembe, ndi achuma, ndi amphamvu, ndi akapolo onse, ndi mfulu, anabisala kumapanga, ndi matanthwe a mapiri;

"nanena kwa mapiri ndi matanthwe, Igwani pa ife, ndipo tibiseni ife ku nkhope ya Iye amene akhala pa mpando wachifumu, ndi ku mkwiyo wa Mwanawankhosa; chifukwa lafika tsiku lalikuru la mkwiyo wao, ndipo akhoza kuima ndani?" Chibvumbulutso 6:15-17.

"Ndipo ndinaona chirombocho, ndi mafumu a dziko, ndi magulu a nkhondo ao, osonkhanidwa kuchita nkhondo pa Iye wakukwera pa kavalo, ndi gulu la nkhondo lake. Ndipo chinagwidwa chirombocho, ndi pamodzi nacho mneneri wonyenga amene adachita zizindikilo pamaso pake, zimene anasokeretsa nazo iwo amene adalandira lemba la chirombo, ndi iwo akulambira fano lake; iwo awiri anaponyedwa ali moyo m'nyanja yamoto yakutentha ndi sulfure." Chibvumbulutso 19:19-20.

"Ndipo akuphedwa a Yehova adzakhala tsiku lomwelo kuchokera ku malekezero ena a dziko lapansi kunka ku malekezero ena a dziko lapansi, sadzaliridwa maliro, sadzasonkhanidwa, sadzaikidwa; adzakhala ngati ndowe pa nthaka." Yeremiya 25:33.

## Mulungu mwa Chikondi Adzasamala Onse Amene Adalira ndi Kummvera Iye.

"Sadzaopa choopsa cha usiku, kapena mubvi wopita usana; kapena mliri woyenda mumdima, Kapena chionongeko chakuthera usana.

"Pambali pako padzagwa chikwi, ndi zikwi khumi pa dzanja lamanja lako; Sichidzakuyandikira iwe….

"Popeza udati, Inu Yehova, ndinu pothawirapo panga! Udaika Wam'mwambamwamba chokhalamo chako; palibe choipa chidzakugwera, ndipo cholanga sichidzayandikiza hema wako." Masalmo 91:5-7, 9-10.

"Zitatha izi ndinaona angelo anai alikuimirira pa ngondya zinai za dziko, akugwira mphepo zinai za dziko, kuti ingaombe mphepo pa dziko, kapena pa nyanja, kapene pa mtengo uli wonse.

"Ndipo ndinaona mngelo wina, anakwera kuchokera poturuka dzuwa, ali nacho chizindikilo cha Mulungu wamoyo: ndipo anapfuula ndi mau akuru kuitana angelo anai, amene adalandira mphamvu yakuipsa dziko ndi nyanja,

"nanena, Musaipse dziko, kapena nyanja, kapena mitengo, kufikira tidasindikiza chizindikiro akapolo a Mulungu wathu, pamphumi pao." Chibvumbulutso 7:1-3.

"Sadzamvanso njala, kapena ludzu, kapena silidzawatentha dzuwa, kapena chitungu chiri chonse; chifukwa Mwanawankhosa wakukhala pakati pa mpando wachifumu adzawaweta, nadzawatsogolera ku akasupe a madzi a moyo, ndipo Mulungu adzawapukutira misozi yonse pamaso pao." Chibvumbulutso 7:16-17.

"Idzani, anthu anga, lowani m'zipinda mwanu, nimutseke pamakomo panu; nimubisale kanthawi kufikira mkwiyo utapita. Pakuti taonani, Yehova adza kuchokera ku malo ake kudzazonda okhala pa dziko lapansi, chifukwa cha kuipa kwao; dziko lidzabvumbulutsa mwazi wake, ndipo silidzabvundikiranso ophedwa ake." Yesaya 26:20-21.

"Ndipo ndinaona chizindikilo china m'mwamba, chachikuru ndi chozizwitsa, angelo asanu ndi awiri akukhala nayo miliri isanu ndi iwiri, ndiyo yotsiriza, kuti mwa iyo watsirizika mkwiyo wa Mulungu.

"Ndipo ndinaona ngati nyanja ya mandala yosanganiza ndi moto; ndipo iwo amene anachilaka chirombocho, ndi fano lake ndi chiwerengero cha dzina lake anaimirira pa nyanja ya mandala, nakhala nao azeze a Mulungu.

"Ndipo ayimba nyimbo ya Mose kapolo wa Mulungu, ndi nyimbo ya Mwanawankhosa, nanena, Ntchito zanu nzazikuru ndi zozizwitsa, Ambuye Mulungu, Wamphamvu yonse; njira zanu nzolungama ndi zoona, Mfumu Inu, ya nthawi zosatha." Chibvumbulutso 15:1-3.

"Ndipo chinjoka chinakwiya ndi mkazi, nichinachoka kunka kuchita nkhondo ndi otsala a mbeu yake, amene asunga malamulo a Mulungu, nakhala nao umboni wa Yesu." Chibvumbulutso 12:17.

"Ndipo nthawi yomweyi adzauka Mikaeli kalonga wamkuru wakutumikira ana a anthu a mtundu wako; ndipo padzakhala nthawi ya masautso, siinakhala yotere kuyambira mtundu wa anthu kufikira nthawi yomwe ija; ndipo nthawi yomweyo anthu ako adzapulumutsidwa, yense amene ampeza wolembedwa m'bukhu.

"Ndipo ambiri a iwo ogona m'pfumbi lapansi adzauka, ena kumka ku moyo wosatha, ndi ena ku manyazi ndi mnyozo wosatha." Danieli 12:1-2.

"Mkati mwakugwedezeka kwa dziko lapansi, kung'anima, ndi kugunda kwa mphenzi, liu la Mwana wa Mulungu liitana oyera mtima anagonawo kuti auke. Ayang'anitsitsa maso ake pa manda pa olungama, nakweza manja ake kumwamba, napfuuka: "Ukani, Ukani, Ukani, inu amene mugona m'fumbi nyamukani!' Kuchokera mu ndende ya imfa iwo auka, atabvala chosabvunda cha ulemelero, akupfuula, 'Imfawe, chigonjetso chako chiri kuti? Imfawe, mbola yako iri kuti?' 1 Akorinto 15:55." The Great Controversy, 644.

"Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka;

"pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse." 1 Atesalonika 4:16-17.

"Iye wakuchitira umboni izi anena, Indetu; ndidza msanga. Amen; idzani, Ambuye Yesu." Chibvumbulutso 22:20.

"Wodala ndi woyera mtima ali iye amene achita nao pa kuuka koyamba... komatu adzakhala ansembe a Mulungu ndi a Khristu, nadzachita ufumu pamodzi ndi Iye zaka chikwizo." Chibvumbulutso 20:6.

"Ndipo ndinaona m'mwamba mwatsopano ndi dziko latsopano; pakuti m'mwamba moyamba ndi dziko loyamba zidachoka, ndipo kulibenso nyanja.

"Ndipo ndinaona mzinda woyerawo, Yerusalemu watsopano, ulikutsika Kumwamba kwa Mulungu, wokonzeka ngati mkwatibwi wokometsedwera mwamuna wake.

"Ndipo ndinamva mau akuru ochokera ku mpando wachifumu, ndi kunena, Taonani, chihema cha Mulungu chiri mwa anthu; ndipo adzakhalitsa nao, ndi iwo adzakhala anthu ake, ndi Mulungu yekha adzakhala nao, Mulungu wao;

"Ndipo adzawapukitira misozi yonse kuichotsa pamaso pao; ndipo sipadzakhalanso imfa; ndipo sipadzakhalanso maliro, kapena kulira, kapena chowawitsa; zoyambazo zapita.

"Ndipo Iye wakukhala pa mpando wachifumu anati, Taonani, ndichita zonse zikhale zatsopano. Ndipo ananena, Talemba; pakuti mau awa ali okhulupirika ndi oona." Chibvumbulutso 21:1-5.

"Pomwepo Mfumuyo idzanena kwa iwo a ku dzanja lake la manja, Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, lowani mu ufumu wokonzedweratu kwa inu pa chikhazikiro chake cha dziko lapansi." Mateyu 25:34.

## Chikondi cha Mulungu

Kodi Mulungu amanenedwa kuti ali chiyani?

"Mulungu ndiye chikondi." 1 Yohane 4:8.

Chikondi cha Mulungu za dziko lapansi ndi chachikuru bwanji?

"Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha." Yohane 3:16.

Pakuchita chiyani pomwe Mulungu anachionetsara chikondi chake chopanda malire'chi?

"Umo chidaonekera chikondi cha Mulungu mwa ife, kuti Mulungu anamtuma Mwana wake wobadwa yekha, alowe m'dziko lapansi, kuti tikhale ndi moyo mwa Iye." 1 Yohane 4:9.

Ndi kwa anthu ochuruka bwanji omwe Mulungu amatsanulira madalitso ake?

"Chifukwa Iye amakwezera dzuwa lake pa oipa ndi abwino, nabvumbitsira mvula pa olungama ndi pa osalungama." Mateyu 5:45.

## KUPEMBEDZA MU MPINGO WA M'NYUMBA

Kabukhu aka kakukupatsani uthenga wakuti dziko lapansi, makamaka kumbali ya Chikhristu, posachedwapa pakhazikitsidwa lamulo loletsa kugwira ntchito pa Sunday (tsiku loyamba la pa mlungu) ndi kuyamba kupembedza pa tsiku losakhala la ulamuliro a m'Bukhu Lopatulika koma lokhazikitsidwa ndi Papa. Ngati mudzabvomereza, mudzalandira chizindikilo cha themberero, Lemba la Chirombo pa mphumi panu. Koma ngati mudzapembedza pa Sabata (Saturday) la tsiku la chisanu ndi chiwiri, lomwe ndi lotikumbutsa mphamvu ya Mulungu yakulenga zonse monga lafotokozedwa mu lamulo la chinai la Malamulo Khumi (Eks. 20:8-11) (Gen. 2:1-3), mudzalandira chizindikilo cha lonjezano cha Mulungu pa mphumi panu ndi kudzakhala ndi Iye kwa myaya Kumwamba. Pano mipingo yambiri, abusa ndiponso anthu ambiri ayamba kumvetsetsa ndi kutembenukira ku uthenga wolalikidwa mwa chindunji ndi kabukhu aka ndipo akulimbika mtima pomvera ndi kuchita malamulo a Mulungu omwe tinalamulidwa kuwachitawa. Ngati mutalalikira uthenga uwu ku mpingo wanu ndi kuona kuti sufuna kuchita malamulo a Mulungu'wa, musazengereze dzipatuleni kuturuka m'Babulo (Chibv. 18) popembedza m'nyumba zanu. Itanani mabanja ena, abwenzi, ndi anansi ndi kukhazikitsa timagulu tating'ono ta okhulupirira omwe mungathe kumagawana nao malangizo ofunikira awa ndi kukhala m'modzi wa iwo akubwezeranso Malamulo Khumi a Mulungu omwe anaswedwa. Mosataya nthawi, pemphani ndipo mudzalandira lonjezano la Khristu lakuti: "Pakuti kumene kuli awiri kapena atatu osonkhanira m'dzina langa, ndiri komweko pakati pao." Mateyu 18:20.

Ponena za chikondi chachikuru cha Mulungu, ndi mtima wokhazikika tiyembekezere chiyani?

"Iye amene sanatimana Mwana wake wa Iye yekha, koma anampereka chifukwa cha ife tonse, adzalekeranji kutipatsanso ife zinthu zonse kwaulere pamodzi ndi Iye?" Aroma 8:32.

Mu liu limodzi liti momwe khalidwe la Mulungu likufotokozedwa?

"Iye wosakonda sazindikira Mulungu; chifukwa Mulungu ndiye chikondi." 1 Yohane 4:8.

Chikondi cha Mulungu ndi chokhalitsa bwanji?

"Yehova anaonekera kwa ine kale, ndi kuti, Inde, ndakukonda iwe ndi chikondi chosatha; chifukwa chake ndakukonda iwe ndi kukukomera mtima." Yeremiya 31:3.

Ndi chiyani chomwe chingamlekanitse wokhulupirira weniweni ndi chikondi cha Mulungu?

"Pakuti ndakopeka mtima kuti ngakhale imfa, ngakhale moyo, ngakhale angelo, ngakhale maufumu, ngakhale zinthu ziripo, ngakhale zinthu zirinkudza, ngakhale zimphamvu, ngakhale utali, ngakhale kuya, ngakhale cholengedwa china chiri chonse, sichingakhoze kutisiyanitsa ife ndi chikondi cha Mulungu, chimene chiri mwa Khristu Yesu Ambuye athu." Aroma 8:38-39.

Ndi kwa ndani komwe oyera mtima adzakhala akupereka ulemu wao ku nthawi za myaya?

"Kwa Iye amene atikonda ife, natimasula ku machimo athu ndi mwazi wake,....kwa Iye kukhale ulemelero ndi mphamvu kufikira nthawi za nthawi." Chibvumbulutso 1:5-6.

Kodi chifundo chakuya cha Mulungu chimafotokozedwa bwanji?

"Koma Inu, Ambuye, ndinu Mulungu wansoni ndi wachisomo, wosapsa mtima msanga, ndi wochurukira chifundo ndi choonadi." Masalmo 86:15.

Ndi chifukwa chiyani Ambuye Yesu anatiuza kuti tidzikonda adani athu?

"Koma Ine ndinena kwa inu, Kondanani nao adani anu, ndi kupempherera iwo akuzunza inu; kotero kuti mukhale ana a Atate wanu wa Kumwamba; chifukwa Iye amakwezera dzuwa lake pa oipa ndi pa abwino, namabvumbitsira mvula pa olungama ndi osalungama." Mateyu 5:44-45.

## Ora la Chiweruziro cha Mulungu

Ndi uthenga wodzidzimutsa woti chiyani womwe ukuperekedwa m'Chibvumbulutso 14:7?

"Opani Mulungu, mpatseni ulemelero; pakuti yafika nthawi ya chiweruziro chake; ndipo mlambireni Iye amene analenga m'mwamba ndi mtunda ndi nyanja ndi akasupe amadzi."

Kodi ora la chiweruziro cha Mulungu'li likuchitika liti?

"Nati kwa ine, Mpaka masiku zikwi ziwiri mphambu mazana atatu usana ndi usiku; pamenepo malo opatulika adzayesedwa olungama." Danieli 8:14.

Dziwani ichi: Tsiku la chitetezero la Ayuda limakhala pa tsiku la khumi la mwezi wa chisanu ndi chiwiri, iyi ndi nthawi yomwe kachisi amayeretsedwa. Tsiku la chitetezero'li, kwa Auyda limatengedwa ngati tsiku la chiweruziro, limatengedwa kuti ndi la chiweruziro chakufufuza kumwamba. Zaka 2,300, malingana ndi ulauli zikufikira mpaka nthawi ya kuyeretsa kachisi m'mwamba, kapena mwachidule kungoti chiweruziro chakufufuza. Utumiki wa mkachisi wa Ayuda ukukwaniritsidwa kotheratu mu ntchito ya Khristu. Monga momwe tsiku lakuyeretsedwa kwa Kachisi la nthawi imeneyo linalinso la chiweruziro, chomwecho ntchito yakuyeretsa Kachisi ya Khristu, iphatikiza mkati mwake kufufuza kwa milandu ya anthu ake Iye asanabwere kachiwiri kudzawalandira iwo kwa Iye mwini.

Ndi chitsimikizo chanji chomwe ife tiri nacho kuti chiweruzo chidzachitika osalephera?

"Mulungu...anapangiratu tsiku limene adzaweruza dziko." Machitidwe 17:30-31.

Kodi mu nthawi ya Paulo, chiweruziro chinali mu nthawi ya mtsogolobe?

"Ndipo m'mene anamfotokozera za chilungamo, ndi chidziletso, ndi chiweruziro chirinkudza, Felike anagwidwa ndi mantha." Machitidwe 24:25.

Anthu onse adzaweruzidwa kuchokera m'chiyani?

"Ndipo mabuku anatsegulidwa; ndipo buku lina linatsegulidwa, ndilo la moyo; ndipo akufa anaweruzidwa mwa zolembedwa m'mabuku, monga mwa ntchito zao." Chibvumbulutso 20:12.

"Opani Mulungu, mpatseni ulemelero; pakuti yafika nthawi ya chiweruziro chake." Chibvumbulutso 14:7.

Dziwani izi: Pali magawo atatu a chiweruziro omwe akutchulidwa m'Bukhu Lopatulika: chiweruziro chakufufuza chomwe chikuchitika patsogolo pa Kubwera Kwachiwiri; chiweruzo chotsimikizira za kuipa kwa angelo ndi anthu odziyenereza chomwe chidzachitidwa ndi Khristu pamodzi ndi anthu oyera mtima m'zaka chikwi pambuyo pa Kubwera Kwachiwiri; ndi chiweruziro chotsiriza chomwe chidzachitika pa oipa chomwe chidzakhala mapeto a kuipa. Chiweruzo chakufufuza chikuchitika kumwamba Khristu asanabwere Kachiwiri ndi cholinga chofuna kutsimikizira za iwo amene ali oyenera kudzaukitsidwa pa kuuka koyamba, komanso za amoyo pomwe adzasinthidwe pa kuthwanima kwa diso pa kulira kwa lipenga lotsiriza. Nkofunikira kuti ichi chichitikiretu patsogolo pa Kubwera Kwachiwiri, chifukwa sipadzakhalanso nthawi kuti ichi chidzachitike pakati pa kubwera kwa Khristuko ndi kuukitsidwa kwa akufa kwa olungama anafa kalewo. Chiweruziro chotsiriza cha oipa chidzachitika pambuyo pa milandu yao itaweruzidwa ndi Khristu ndiponso kutsimikizidwa ndi anthu olungama mu nthawi ya zaka chikwi. Werengani Chibvumbulutso 20:4-5; 1 Akorinto 6:1-3. Chiweruziro chakufufuza




Malinga ndi ulosi wa Danieli, zaka 2,300 zinayambira pa "kuturuka lamulo lakukonzanso, ndikumanga Yerusalemu kufikira nthawi yakuyeretsedwa kwa kachisi.

457 B.C. – Ahaswero, mfumu ya Aperezi, analamulira kuti Yerusalemu akonzedwe ndi kumangidwanso. (Danieli 9:24: Ezra 6:1,6-12). Ichi chinali chiyambi cha zaka 2,300.

408 B.C. – Kukonzedwa ndi kumangidwanso kwa Yerusalemu kunachitika zaka 49 zoyambirira za ulosi wa utali wa Danieli'wu. Ntchitoyo inatsirizika mu 408 B.C. (Danieli 9:25).

A.D. 27 – Yesu atadzozedwa ndi Mzimu Woyera ku ubatizo wake, anayamba kulalikira ndi kuphunzitsa. Werengani Mateyu 3:16; Machitidwe 10:38. Kuchokera chaka cha 457 kufika pa Khristu "wodzozedwa" zinakwana zaka 483.

A.D. 31 – Mesiya "analeketsa nsembe yophera pakati pa sabata," pa chaka cha A.D. 31, zitatha zaka zitatu ndi theka za utumiki wake wopambana. Werengani Dan. 9:27; Mateyu 27:50-51. Zaka zotsala zitatu ndi theka za sabata yotsiriza ya masaba makumi asanu ndi ndi ichi chomwe chikulalikidwa ku dziko lapansi mu uthenga wa mngelo wa pa Chibvumbulutso 14:6-7.

Khristu monga Nkhoswe ya anthu ake, adzabvomereza chiyani pamaso pa Atate ndi angelo ake?

"Iye amene alakika adzambveka motero zobvala zoyera; ndipo sindidzafafaniza ndithu dzina lake m'bukhu la moyo, ndipo ndidzambvomereza dzina lake pamaso pa Atate wanga, ndi pamaso pa angelo ake." Chibvumbulutso 3:5. Werengani Mateyu 10:32-33; Marko 8:38.

Dziwani ichi: Panthawi ya chiweruziro iyi onse akufa olungama ndi ochimwa adzakhala ali chikhalire m'manda mwao. Paja ntchito za munthu ali yense zinalembedwa m'mabuku a kumwamba.

## Kubwera Kwachiwiri kwa Khristu

Ndi lonjezano lanji lomwe Khristu anapanga ponena za kubweranso kwake?

"Mtima wanu usabvutike; mukhulupirira Mulungu, khulupirirani Inenso. M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ngati sikudali kotero, ndikadakuuzani inu; pakuti ndipita kukukonzerani inu malo. Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso" Yohane 14:1-3.

Pongomalizika zizindikilo za kubwera kwa Khristu chidzachitikanji?

"Ndipo pamenepo adzaona Mwana wa munthu alinkudza m'mitambo ndi mphamvu ndi ulemelero waukuru." Luka 21:27.

Kodi kukambirana za mtendere wa dziko lapansi kudzapangitsa anthu kukhala mu ntambasale?

"Masiku otsiriza adzafika onyoza ndi kuchita zonyoza, oyenda monga mwa zilakolako za iwo eni, ndi kunena, Liri kuti lonjezano la kudza kwake? Pakuti kuyambira kuja makolo adamwalira zonse zikhala monga chiyambire chilengedwe." 2 Petro 3:3-4.

"Pakuti inu nokha mudziwa bwino kuti tsiku la Ambuye lidzadza monga mbala usiku. Pamene angonena, Mtendere ndi mosatekeseka, pamenepo chiononongeko chobukapo chidzawagwera...Koma inu, abale, simuli mumdima, kuti tsikulo likakugwereni monga mbala." 1 Atesalonika 5:2-4.

Pakukwera kwa Khristu kumwamba, angelo anati chiyani za kubweranso kwake?

"Ndipo pakukhala iwo chipenyerere kumwamba pomuka Iye, taonani amuna awiri obvala zoyera anaimirira pambali pao; amenenso anati, Amuna a ku Galileya muimiranji ndi kuyang'ana kumwamba? Yesu amene walandiridwa kunka Kumwamba kuchoka kwa inu, adzadza momwemo monga munamuona alinkupita Kumwamba." Machitidwe 1:10-11.

Kodi ndi anthu onse okhala pa dziko lapansi omwe adzakhale okonzeka kukumana naye pakubweranso kwake?

"Taonani, adza ndi mitambo; ndipo diso liri lonse lidzampenya Iye, iwonso amene anampyoza; ndipo mafuko onse a pa dziko adzamlira Iye." Chibvumbulutso 1:7. "Ndipo mafumu a dziko, ndi akuru ...anabisala kumapanga, ndi matanthwe a mapiri; nanena...Igwani pa ife, ndipo tibiseni ife ku nkhope ya Iye amene akhala pa mpando wachifumu, ndi ku mkwiyo wa Mwanawankhosa." Chibvumbulutso 6:15-16.

Nthawi yakubwera kwa Khristu idzakhala yolandira mphotho?

"Pakuti Mwana wa munthu adzabwera mu ulemelero wa Atate wake, pamodzi ndi angelo ake; ndipo pomwepo Iye adzabwezera kwa anthu onse monga machitidwe ao." Mateyu 16:27. "Taonani, ndidza msanga; ndipo mphotho yanga ndiri nayo yakupatsa yense monga mwa ntchito yake." Chibvumbulutso 22:12.

Ndi kwa ndani kwalonjezedwa chipulumutso pakuonekera m'mitambo kwa Khristu?

"Koteronso Khristunso ataperekedwa nsembe kamodzi kukasenza machimo a ambiri, adzaonekera pa nthawi yachiwiri, wopanda uchimo, kwa iwo amene amlindira, kufikira chipulumutso." Ahebri 9:28.

Kodi chiyembekezo chotere chiri ndi chikoka chanji pa moyo wa munthu ali yense?

"Tidziwa kuti, pa kuoneka Iye, tidzakhala ofanana ndi Iye, pakuti tidzamuona Iye monga ali. Ndipo yense wakukhala nacho chiyembekezo ichi pa Iye, adziyeretsa yekha, monga Iyeyu ali woyera." 1 Yohane 3:2-3.

Kodi ndi liti pomwe Paulo adzalandire korona?

"Chotsalira wandiikira ine korona wa chilungamo, amene Ambuye, woweruza wolungama, adzandipatsa ine tsiku lijalo: ndipo si kwa ine ndekha, komatunso kwa onse amene anakonda maonekedwe ake." 2 Timoteo 4:8.

## Momwe Khristu Adzabwerere

Pakukwera kwake kumwamba, angelo anati Khristu adzabweranso bwanji?

"Ndipo m'mene adanena izi, ali chipenyerere iwo, ananymulidwa; ndipo mtambo unamlandira Iye kumchotsa kumaso kwao. Ndipo pakukhala iwo chipenyerere kumwamba pomuka Iye, taonani, amuna wiri obvala zoyera anaimirira pambali pao; amenenso anati, Amuna a ku Galileya, muimiranji ndi kuyang'ana kumwamba? Yesu amene walandiridwa kunka Kumwamba kuchokera kwa inu, adzadza momwemo monga munamuona alinkupita Kumwamba." Machitidwe 1:9-11.

Nanga Khristu anati madzedwe ake a dzakhala otani?

"Pakuti Mwana wa munthu adzabwera mu ulemelero wa Atate wake, pamodzi ndi angelo ake." Mateyu 16:27. "Ndipo pomwepo padzaoneka m'thambo chizindikilo cha Mwana wa munthu; ndipo mitundu yonse ya pa dziko lapansi idzadziguguda pachifuwa, nidzapenya Mwana wa munthu alinkudza pa mitambo ya kumwamba, ndi mphamvu ndi ulemelero waukuru." Mateyu 24:30.

Nanga Khristu anatichenjeza motani za ziphunzitso za aneneri onyega?

"Pomwepo munthu akanena kwa inu, Onani, Khristu ali kuno, kapena uko musambvomereze; chifukwa Akhristu onama adzauka, ndi aneneri onama nadzaonetsa zizindikilo zazikuru ndi zozizwa: kotero kuti akanyenge, ngati




awiri ikutifikitsa ife pafupifupi penipeni pa mapeto a nthwai ya zaka mazana anai kudza makumi asanu ndi anai yomwe inalamulidwa pa mtundu wa anthu a Chiyuda.

A.D. 34 – Kuponyedwa miyala kwa Stefano. Kuchokera pamenepo Uthenga unapita kwa amitundu Werengani Dan. 9:24; Machitidwe 7:54-58; 8:1. Kuyambira chaka cha 457 kufika "pa uthenga kwa amitundu" zinakwanira zaka 490 kapena kuti masabata makumi asanu ndi awiri.

A.D. 1844 – Uthenga wa angelo atatu wa Chibvumbulutso 14:6-12 udayamba kulalikidwa pa dziko lapansi patangotsala pang'ono kuti Khristu abwere kachiwiri.

A.D. 1844 – Mapeto a zaka 2,300. Ndi nthawinso ya kuyeretsedwa kwa kachisi mu nthawi ya chiweruziro cha Mulungu.

nkotheka, osankhidwa omwe. Onani ndakuuziranitu pasanafike. Chifukwa chake akanena kwa inu, Onani Iye ali m'chipululu; musamukeko. Onani, ali m'zipinda musabvomereze." Mateyu 24:23-26.

Kudza kwake, Kudzakhala koonekera bwanji?

"Pakuti monga mphenzi idzera kum'mawa, nionekera kufikira kumadzulo; kotero kudzakhalanso kufika kwake kwa Mwana wa munthu." Ndime 27.

Chidzachitika chiyani pa kulira kwa lipenga?

"Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka." 1 Atesalonika 4:16.

Ndi kulekanitsa kwa chiyani komwe kudzachitike akadzabwera Yesu?

"Koma pamene Mwana wa munthu adzadza mu ulemelero wake, ndi angelo onse pamodzi naye, pomwepo Iye adzakhala pa chimpando cha kuwala kwake: ndipo adzasonkhanidwa pamaso pake anthu a mitundu yonse; ndipo Iye adzalekanitsa iwo wina ndi mnzake, monga mbusa alekanitsa nkhosa ndi mbuzi." Mateyu 25:31-32.

Adzati chiyani kwa iwo a kudzanja lake lamanja?

"Pomwepo Mfumuyo idzanena kwa iwo a ku dzanja lake lamanja, Idzani kuno inu odalitsika a Atate wanga, lowani mu Ufumu wokonzedwera kwa inu pa chikhazikiro chake cha dziko lapansi. Ndime 34.

Nanga kwa iwo a ku lamanzere adzati chiyani?

"Pomwepo Iye adzanena kwa iwo a ku dzanja lamanzere, Chokani kwa Ine otembereredwa inu, ku moto wa nthawi zonse wokonzedwera mdierekezi ndi amithenga ake." Ndime 41.

Nanga kwa anthu ake Mulungu adzakhala chiyani?

"Ndipo Yehova adzadzuma ali ku Ziyoni, ndi kumveketsa mau ake ali ku Yerusalemu; ndi thambo ndi dziko lapansi zidzagwedezeka; koma Yehova adzakhala chopulumukirako anthu ake, ndi linga la ana a Israyeli." Yoweli 3:16. Werengani Yeremiya 25:30-31; Hagai 2:21; Ahebri 12:26; Masalmo 91:5-10.

Nanga Paulo akukufotokoza bwanji kubwera kumeneku?

"Kotero Khristunso ataperekedwa nsembe kamodzi kusenza machimo a ambiri, adzaonekera pa nthawi yachiwiri, wopanda uchimo, kwa iwo amene amlindirira kufikira chipulumutso." Ahebri 9:28.

Ndi lemba liti lomwe likufotokoza mwatchutchutchu za zaka chikwi za chiweruziro?

"Ndipo ndinaona mipando yachifumu, ndipo anakhala pamenepo; ndipo anawapatsa chiweruziro…ndipo anakhala ndi moyo nachita ufumu pamodzi ndi Khristu zaka chikwi." Chibvumbulutso 20:4.

Chidzachitika chiyani kwa oipa amoyo pamene Khristu adzabwera?

"Ndipo monga kunakhala masiku a Nowa, momwemo kudzakhalanso masiku a Mwana wa munthu. Anadya, anamwa, anakwatira, anakwatiwa, kufikira tsiku lija Nowa analowa m'chingalawa, ndipo chinadza chigumula,ndi chinaononga onsewo; momwenso kunakhala masiku a Loti… tsiku limene Loti anaturuka m'Sodomu udabvumba moto ndi sulfure zochokera kumwamba, ndipo zinaononga onsewo; momwemonso kudzakhala tsiku lakumbvumbuluka." Luka 17:26-30.

## Kuyamba kwa zaka Chikwi

Kodi pali midzukilo ingati?

"Musazizwe ndi ichi, kuti ikudza nthawi, imene onse ali m'manda adzamva mau ake, nadzaturukira, amene adachita zabwino, kukuuka kwa moyo; koma amene adachita zoipa kukuuka kwa kuweruza." Yohane 5:28-29.

Kodi ndi gulu liti lokhalo lomwe lidzatenga nawo mbali pa kuuka koyamba?

"Wodala ndi woyera mtima ali iye amene achita nao pa kuuka koyamba; pa iwowa imfa yachiwiri iribe ulamuliro." Chibvumbulutso 20:6.

## Chiyambi cha zaka Chkwi

1. Kutha kwa miliri isanu ndi iwiri
2. Kubwera kwachiwiri kwa Khristu
3. Olungama akufa aukitsidwa
4. Oipa afa, Satana amangidwa
5. Oyera mtima akwera Kumwamba

## Kutha kwa zaka Chikwi

1. Yesu ndi oyera mtima atsika kumwamba
2. Mzinda Woyera utsika
3. Oipa akufa aukitsidwa
4. Satana amasulidwa
5. Oipa aonongedwa

Zaka chikwi ndi nthawi yotsiriza ya Mulungu – nthawi yaikuru ya sabata la zaka 1000 lakupumula kwa dziko lapansi ndi kwa anthu a Mulungu atadutsa m'mabvuto ndi m'zochitikachitika kwa zaka 6,000 mu mbiri ya dzko lapansi.

Ikangotha ntchito ya uthenga wabwino, pambuyo pafika Ufumu wa muyaya wa Mulungu pano pa dziko lapansi.

Nthawi imeneyi ikuphatikiza mkati mwake chinthu chija chomwe Bukhu Lopatulika lakhala likunena za icho kuti "tsiku la Ambuye."

Kumayambiriro ndi kumapeto ake nthawi'yi iri ndi midzukiro.

Kumayambiriro kwake kuli kutsanuridwa kwa miliri isanu ndi iwiri yotsiriza, kubwera kwachiwiri kwa Khristu, kuukitsidwa kwa olungama akufa, kumangidwa kwa Satana, kusinthika ndi kukwera kumwamba kwa olungama; kumapeto a nthawiyo kuli, kutsika kwa Yerusalemu Watsopano, ndi Khristu ndiponso olungama kuchokera kumwamba, kuukitsidwa kwa akufa osalungama, kumasulidwa kwa Satana, ndi chiononngeko chotsiriza cha osalungamawo.

Mu nthawi ya zaka chikwi'yi dziko lapansi lidzakhala lopasuka; Satana ndi angelo ake adzakakamizika kukhala m'dziko lopasuka'li; pamene olungama pamodzi ndi Khristu, adzakhala ali pa chiweruziro cha osalungama chakuloza ku chilango chao chotsiriza.

Kenaka akufa osalungama adzaukitsidwa; Satana adzamasulidwa kwa kanthawi kochepa, ndipo iye ndi gulu la osalungama'lo adzazungulira msasa wa olungama ndi Mzinda Woyerawo. Ndipo moto udzatsika pansi kuchokera kumwamba kwa Mulungu ndi kuwanyeketsa iwo. Dziko lapansi lidzayeretsedwa ndi moto womwe udzanyeketse osalungamawo. Dziko lapansi lolengedwa mwatsopano lidzakhala kwao kwa olungama.

Zaka chikwi ndi nthawi yomwe imadziwikanso kuti "zaka zirinkudza." Kutha kwa nthawi imeneyi kudzakhala chiyambi cha ulamuliro ndi dziko latsopano.

# Taonani Ali Nkudza



Kukhaliranso pamodzi kwa banja kumwamba

Ndi nthawi yotalika bwanji yomwe Satana adzamangidwa pa dziko lapansi pano?

“Ndipo ndinaona mngelo anatsika Kumwamba, nakhala nacho chifungulo cha pompho, ndi unyolo waukuru m’dzanja lake. Ndipo anagwira chinjoka, njoka yakaleyo, ndiye mdierekezi ndi Satana, nammanga iye zaka chikwi, namponya ku phompho, natsekapo, nasindikizapo chizindikilo pamwamba pake, kuti asanyengenso amitundu kufikira kudzatha zaka chikwi.” Chibvumbulutso 20:1-3.

Pafupi pakutha kwa zaka chikwi undende wa Satana udzasinthidwa bwanji?

“Patsogolo pake ayenera kumasulidwa iye kanthawi.” Ndime 3.

Olungama akufa adzaukitsidwa pa kubwera kwachiwiri kwa Khristu. Nanga akufa onse, osalungama adzauka liti?

“Otsala a akufa sanakhalanso ndi moyo kufikira kudzatha zaka chikwi.” Ndime 5.

Akadzangoukitsidwa akufa oipa mwamsangamsanga Satana adzapitirizanso kuchita chiyani?

“Ndipo pamene zidzatha zaka chikwi, adzamasulidwa Satana m’ndende yake; nadzaturuka kudzasokeretsa amitundu ali mu ngondya zinai za dziko, Gogi ndi Magogi, kuwasonkhanitsa achite nkhondo: chiwerengero chao cha iwo amene chikhala ngati mchenga wa kunyanja.” Ndime 7-8.

Oipa’wa adzachita nkhondo ndi ndani, nanga Chotsatira chake chidzakhala chiyani?

“Ndipo anakwera nafalikira m’dziko, nazinga tsasa la oyera mtima ndi mudzi wokondedwawo; ndipo unatsika moto wakumwamba nuwanyeketsa.” Ndime 9.

Osalungama adzakhala motani kwa muyaya?

“Amene adzamva chilango, ndipo chionongeko chosatha chiwasiyanitsa ku nkhope ya Ambuye.” 1 Atesalonika 1:9.

## Kwao kwa Opulumutsidwa

Kodi dziko lapansi linapangidwa kukhala lokhalamo ndani?

“Pakuti atero Yehova amene analenga kumwamba, Iye ndiye Mulungu amene anaumba dziko lapansi, nalipanga; Iye analikhazikitsa, sanalilenga mwachabe; Iye analiumba akhalemo anthu.” Yesaya 45:18.

Ndi kwa ndani komwe Mulungu analipereka dziko lapansi?

“Kunena za Kumwamba, kumwamba ndiko kwa Yehova; Koma dziko lapansi analipereka kwa ana a anthu.” Masalmo 115:16.

Kodi munthu analengedwa kuchita chiyani?

“Mudamchititsa ufumu pa ntchito za manja anu; Mudagonjetsa zonse pansi pa mapazi ake.” Masalmo 8:6.

Pamene munthu anataya ulamuliro wake, unatengedwa ndi ndani?

“Pakuti iye amene munthu agonjetsedwa naye, ameneyonso adzakhala kapolo wake.” 2 Petro 2:19.

Dziwani ichi: Munthu anagonjetsedwa ndi Satana m’Munda wa Edeni, pakutero anadzipereka yekha kukhala kapolo wa womgonjetsayo.

Pamene ankamuyesa Khristu, Satana anadzionetsa ngati kuti ali mwini chiyani?

“Ndipo m’mene anamtsogolera anakwera naye, namuonetsa Iye maufumu onse a dziko lokhalamo anthu, m’kamphindi kakang’ono. Ndipo mdierekezi anati kwa Iye, Ine ndidzapatsa Inu ulamuliro wonse umenewu ndi ulemelero wao: chifukwa unaperekedwa kwa ine; ndipo ndiupatsa kwa iye amene ndifuna.” Luka 4:5-6.

Khristu anati anthu ofatsa ali odala chifukwa ninji?

“Odala ali akufatsa; adzalandira dziko lapansi.” Mateyu 5:5.

Yohane anaona chiyani m’masomphenya?

“Ndipo ndinaona m’mwamba mwatsopano ndi dziko latsopano; pakuti m’mwamba moyamba ndi dziko loyamba zidachoka, ndipo kulibenso nyanja.” Chibvumbulutso 21:1.

Kodi zofuna za oyera mtima zidzayankhidwa ndi kupatsidwa bwanji?

“Ndipo padzakhala kuti asanaitane Ine, ndidzayankha; ndipo ali chilankhulire, Ine ndidzamva.” Yesaya 65:24.

Nanga m’dziko latsopano’lo mudzakhala makhalidwe otani?

“Mmbulu ndi mwana wa nkhosa zidzadyera pamodzi; ndi mkango udzadya udzu ngati ng’ombe; ndi pfumbi lidzakhala chakudya cha njoka; sizidzapwetekana, kapena kusakazana m’phiri langa lonse lopatulika, ati Yehova.” Ndime 25.

Ndi nyengo ziti zakupembedza zomwe zidzasungidwanso ku dziko latsopano?

“Pakuti monga m’mwamba mwatsopano ndi dziko lapansi latsopano limene ndidzalenga, lidzakhalabe pamaso pa Ine, ati Yehova, momwemo adzakhalabe ana anu ndi dzina lanu. Ndipo kudzakhala kuti kuyambira pa mwezi wokhala kufikra ku unzake, ndi kuyambira pa Sabata lina kufikira ku linzake, anthu onse adzafika kudzapembedzera pamaso pa Ine, ati Yehova.” Yesaya 66:22-23.

## Yerusalemu Watsopano

Yohane anauona m’maonekedwe otani mzindawo?

“Ndipo ndinaona mzinda woyerawo, Yerusalemu watsopano, ulikutsika Kumwamba kwa Mulungu, wokonzeka ngati mkwatibwi wokometsedwera mwamuna wake.” Chibvumbulutso 21:2.

Mzindawo unali ndi maziko angati?

“Ndipo linga la mudzi linakhala nao maziko khumi ndi awiri, ndi pomwepo maina khumi ndi awiri a atumwi khumi ndi awiri a Mwanawankhosa.” Ndime 14.

Ndi chiyani chomwe sichidzaloledwa kulowa mu mzindawo?

“Ndipo simudzalowa konse momwemo kanthu kali konse kosapatulidwa kapena iye wakuchita chonyansa ndi bodza.” Ndime 27.

Ndi chiyani chidzadutsa mu mzindamo?

“Ndipo anandionetsa mtsinje wa madzi a moyo, wonyezimira ngati krustalo, oturuka ku mpando wachifumu wa Mulungu ndi wa Mwanawankhosa.” Chibvumbulutso 22:1.

Ndi chiyani chiri ku mbali zonse za mtsinjewo?

“Pakati pa khwalala lake, ndi tsidya ili la mtsinje, ndi tsidya lake lija panali mtengo wa moyo wakubala zipatso khumi ndi ziwiri, ndi kupatsa zipatso zake mwezi ndi mwezi; ndipo masamba a mtengo ndiwo akuchiritsa nao amitundu.” Ndime 2.

Yohane akuti miseu ya mzindawo ndi yopangidwa ndi chiyani?

“Ndipo khwalala la mzinda ndi la golidi woyengeka, ngati mandala oonekera.” Chibvumbulutso 21:21.

Ndi chifukwa chiyani simufunika dzuwa kapena mwezi mu mzindamo?

“Ndipo pamzinda sipafunika dzuwa, kapena mwezi wakuuwalira; pakuti ulemelero wa Mulungu uunikira umenewu, ndipo nyali yake ndiye Mwanawankhosa. Ndipo amitundu adzayendayenda mwa kuunika kwake; ndi mafumu a dziko atenga ulemelero wao kulowa nao momwemo.” Ndime 23-24. Werenganinso Chibv. 22:5; Yesaya 60:19-20.

Nanga ndi ndani okha adzaloledwa kulowa mu mzindawo?

“Odala iwo amene atsuka miinjiro yao, kuti akakhale nao ulamuliro pa mtengo wa moyo, ndi kuti akalowe m’mzinda pa zipata.” Chibvumbulutso 22:14.

Mkangano waukuru watha. Tchimo ndi osalungama kulibenso. Chilengedwe chonse ndi choyera. Pali mgwirizano kumbali zonse ndi chimwemwe ndi kukondwera pakati pa zolengedwa zonse. Kuchokera mwa Iye amene analenga zonse, muturuka moyo ndi kuunika ndi chimwemwe, zomwe zifalikira konsekonse kumwamba ndi dziko lapansi. Kuyambira pa kacholengedwa kakang’no kwambiri, kufikira zazikuruzikuru ngati dziko lapansi, zinthu zonse zamoyo ndi zopanda moyo, mu chilengedwe chao changwiro ndi chokoma, zilalikira kuti Mulungu ali chikondi.” Great Controversy, 678.


MUKAFUNA KUMVA NDI KUDZIWA ZAMBIRI LEMBERANI KU:

**RLMedia**
32 Ceres Str, Comptonville,
Johannesburg, South Africa
www.rlmedia.co.za
+27(0)836254786



View, Read, or Print Books: www.earthsfinalwarning.com
www.sabbathtruth.com
www.worldincrisis.org
www.bible-sabbath.com
www.evolutionfacts.com